



Buku la Mphunzitsi

Nthawiyabaibulo
Kalasi 0, Yoyamba ndi Yachiwiri

Maphunziro A1 - A6

Bible Educational Services

Registered Charity UK (No 1186004)

Cholinga cha Utumiki

Kukonzera ena maphunziro a Baibulo kuti apereke choonadi cha Yesu ku m'bado otsatira pa dziko lonse lapansi.

Masomphenya a Utumiki

Kupereka ku m'bado wotsatira maphunziro okwanira, m'chiyankhulo chawo powalembera ndi kuwathandiza komanso kuthandiza anzathu ena onse odzipereka pa dziko lonse.

ZOYENERA KUDZIWA

Zomwe a Bible Educational Services amachita

A Bible Educational Services (BES UK) amasindikiza maphunziro a “Nthawiyabaibulo”, “Moyo Watsopano” ndi “Okolola” a m'Chingerezi komanso amathandiza a Postal Bible Schools ndi mabungwe ena amene amagwiritsa ntchito maphunziro a BES ku UK ndi ku mayiko a kutsidya la nyanja pokawachezera, kugwira nawo ntchito limodzi, kuwalangiza ndi kuwaphunzitsa. BES imagwiranso ntchito pamodzi ndi magulu ena amene akugwira ntchito yomasulira maphunzirowa m'ziyankhulo zawo, pomasulira, kusindikiza ndi kupereka maphunziro kwa anthu ena. Maphunzirowa amaperekedwa mwaulere kwa ophunzira onse.

Maphunziro a Nthawiyabaibulo anayamba kugwiritsidwa ntchito ku Kumpoto kwa Ireland zake 60 zapitazo. A Bible Educational Services ndi amene ali ndi udindo woyang'anira ntchito yosindikiza maphunzirowa m'Chingerezi ndi m'ziyankhulo zina zonse. Maphunziro a Nthawiyabaibulo amasindikizidwa mu A4 ndipo amathandiza ophunzira m'madera ena kuti masabata anayi aliwonse azitha kutumiza mayankho ku Postal Bible School Centre kuti akachonge. Posachedwapa, tikuyamika a bungwe la Every Home Crusade (Bungwe la Chitsistimutso) ku Belfast, anayamba kusindikiza maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi amene amatchedwa A5. Amenewa amagwiritsidwa ntchito m'matchalichi ndi m'sukulu makamaka ku mayiko akunja kuti akhale osavuta chifukwa kumeneko njira zotumizira ndi zovuta kwambiri.

Maphunziro a BES ndi apadera kwambiri chifukwa amatha kugwiritsidwa ntchito m'nyumba kapena pa gulu (tchalichi kapena sukulu), potsatira ndondomeko imene imalola ophunzira kuphunzira kwa zaka makumi awiri. Gulu lililonse lili ndi maphunziro asanu molingana ndi zaka zawo, Amene sanayambe sukulu (Kalasi 0), zaka 5-7 (Kalasi Yoyamba), zaka 8-10 (Kalasi Yachiwiri), zaka 11-13 (Kalasi Yachitatu), zaka 14-16 (Kalasi Yachinayi). Pali ndondomeko ya kaphunzitsidwe ya zaka zitatu ya gulu lililonse molingana ndi zaka zawo. (Onani peji 4.) Magulu angathe kusintha molingana ndi kuthekera kwawo. A Bibletime Resource amapereka mpata kwa ana kuphunzira Mawu a Mulungu ndi kutha kuzindikira kufunika kwa Uthenga Wabwino pa miyoyo.

Maphunziro akupezeka m'Chingerezi pa BES website – www.besweb.com kapena kuchokera kwa Mlembi Wamkulu. Amapezekanso pa website ya ziyankhulo zina. BES ali ndi zomwe analemba zothandiza amene akufuna kugwira nawo ntchitoyi, ndipo zimenezi zilinso pa website yawo.

Keyala

International and Northern Ireland Secretary (stockist of all English lessons)

Mr S Balmer, BES Office (UK), 37a Belmore Street, Enniskillen, Northern Ireland. BT74 6AA

Phone: 00 44 286 632 2462

Email: sam@besweb.com

UK Secretary – Editorial feedback

Mr Stephen Gillham

Email: stephen.gillham@besweb.com

Web address: www.besweb.com

Email address: info@besweb.com

BUKU LA MPHUNZITSI

Poyamba, maphunziro awa anakonzedwa ndi cholinga choti akhale otumizira anthu, koma lero maphunzirowa akugwiritsidwa ntchito kwambiri pamene njira zotumizira ndi zosadalirika. M'madera ena monga ku mipingo ya ku Afrika, India ndi mayiko ena kulibe njira zotumizira zodalirika. Chifukwa cha ichi, Buku la Mphunzitsi linakonzedwa kuti lithandize amene sangathe kulandira pa positi. Buku la Mphunzitsi m'buku lino ndi la Kalasi 0, Yoyamba ndi Yachiwiri.

Buku la Mphunzitsi lililonse lili ndi ndime zonse zimene zili m'maphunziro a Nthawiyabaibulo. Maphunziro a Nthawiyabaibulo ndi Buku la Mphunzitsi zinakonzedwa kuti zigwire ntchito sabata lililonse. Maphunziro a mwezi wa Epulo amafotokoza za Paska ndipo a mwezi wa Disembala za Khirisimasi.

Madera ena amagwiritsa ntchito maphunziro a pa mwezi otchedwa A4, amene ali ndi maphunziro anayi ndipo ena amagwiritsa ntchito maphunziro otchedwa A5 amene ali ndi maphunziro 24. Mphunzitsi kapena mtsogoleri akuyenera kupereka maphunziro a A4, ndipo sabata lililonse azilemba mayankho a phunzirolo m'tchalichi, ku sukulu kapena ku nyumba ndi kupereka mayankhowo sabata lotsatiralo. Kumapeto kwa mwezi, mphunzitsi kapena mtsogoleri adzilandira maphunzirowo ndi kukachonga, akatsiriza abwere nawo ndi kupereka kwa ophunzirawo.

Ngati ophunzira akugwiritsa ntchito buku, mphunzitsi atenge bukulo kumapeto kwa phunziro lililonse ndi kukachonga. Koma tikudziwa kuti madera ena izi ndi zosatheka. Ngati akuphunzira m'kalasi, ophunzira asinthane mabuku awo ndipo mphunzitsi kapena mtsogoleri awathandize kupeza mayankho ndipo ophunzirawo achongelane maphunziro awo. Kumapeto kwa bukuli kuli malo oyika marikisi amene wophunzira wapeza mwezi uliwonse ndiponso malo a ndemanga ya mtsogoleri ya momwe wophunzirayo akuchitira m'kalasi. Palinso satifiketi yomwe wophunzira ayenera kulandira yoonetsa marikisi ake a maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi.

Timakondwera pamene anthu akutifotokozera zomwe akukumana nazo pogwiritsa ntchito Buku la Mphunzitsi ndi mabuku a Nthawiyabaibulo ndipo tumizani ndemangazo kwa stephen.gillham@besweb.com.

KUKONZEKERA KWA APHUNZITSI

Buku la Mphunzitsi si lotsekeka kuti mphunzitsi sangathenso kuyikapo zinthu zina zomwe akuziona kuti ndi zothandiza pophunzitsa. Nawa malangizo othandiza pogwiritsa ntchito Nthawiyabaibulo.

- **Kudziwa bwino nkhani** - Aphunzitsi akuyenera kudziwa bwino nkhani ya m'Baibulo komanso phunziro la Nthawiyabaibulo lomwe akugwiritsa ntchito. Nkhani ndi yakuti, mphunzitsi awerenge phunzirolo nthawi yophunzitsa isanakwane. Iye amvetse bwino ndondomeko ya phunziro lililonse kuti akonzekere bwino kuphunzitsako.
- **Kumvetza phunziro lokaphunzitsa** - Poyamba pa ndondomeko ya phunziro lililonse pali mawu akuti, "Ife tikuphunzira kuti" motsatidwa ndi zolinga ziwiri zophunzirira zomwe mwina ana angamvetse ngati mphunzitsi atafotokoza, kenaka pali gawo lotsiriza phunziro la Nthawiyabaibulo. Cholinga chophunzirira ndi kufuna kudziwa nkhaniyo, pamene chachiwiri ndi cholimbikitsa ophunzira kuti aganizire zomwe aphunzirazo ndi kuzigwiritsa ntchito pa moyo wawo. Zolinga zimenezi zikugwirizana kwambiri ndi fundo/choonadi cha m'phunzirolo ndipo aphunzitsi akuyenera kugwiritsa ntchito zimenezi kuti adziwe momwe aphunzitsira ndi zomwe ana aphunzira.
- **Mawu oyamba** - Maphunziro onse akuyamba ndi mawu akuti, "kumene kuli ana" ali ndi zomwe akukumana nazo. Pali njira zambiri zomwe tapereka zothandiza ana kutenga mbali pa zokambirana nthawi ya maphunzirowo.
- **Kuphunzitsa** - Fundo zazikulu za phunziro tapereka. Tikuyembekezera kuti aphunzitsi sadzikhalanso akumaziwerenga pamene akuphunzitsa koma kuti akhala atadziwa bwino nkhani yonse ndipo adzitha kufotokoza nkhaniyo mochititsa chidwi. Mphunzitsi ayeseke kuti ana amvetse mitu ya maphunzirowo kuchokera pa nkhani yomwe akuphunzira ndiponso awathandize kumvetsetsa zoyenera kuchita kuchokera mu nkhaniyo. Pamene m'poyenera taye setsa kufotokozera bwino monga nkhani chabe. Mawu amenewa tawalemba motere: **ITALICS.**
- **Kuphunzira** - Nkhani iliyonse ili ndi Vesi Yoloweza. Malo ena muli Mavesi Oloweza awiri; taonjezera vesi ina yomwe tikuona kuti itha kukhala yothandiza kuti ana aphunzire mosavuta. Tikukhulupirira kuti ana adzaphunzira Mavesi Oloweza ndipo aziwakumbukira koterokuti adzadziwa mavesi ambiri.

- **Kutsiriza** - Kwa amene akuphunzira m'kalasi, mphunzitsi ayenera kudziwa ngati ophunzira angathe kutsiriza ntchito yawo ndiponso za thandizo lomwe likufunika kuchokera kwa mphunzitsiyo. Kwa ophunzira ena padzafunika kuti mphunzitsi aziwerenga nkhaniyo, ophunzirawo n'kumatsatira kapena kumvera. Koma enanso adzatha kuwerenga okha nkhaniyo. M'njira zonse ziwiri, ndi kofunika kuwauza malangizo okhudzana ndi mafunso. Ngati Nthawiyabaibulo sikuchitikira m'kalasi, n'kofunika kuti aphunzitsi azipezeka kuti azithandiza kuyankha mafunso osati aziyankha ngati a m'kalasi wamba. Ophunzira ayenera kumasangalala, kulimbikitsidwa ndi kuyamikiridwa pamene kuphunzira.
- **Kukumbutsana** - Zomwe zingatheke chitani, khalani ndi nthawi ya mafunso, ya masewero ndi zina zambiri. Izi zidzathandiza kuphunzira ndi kukumbukira pamtima nkhaniyo.
- **Kuonetsa** - Nthawi zina, zinthu zoti muonetse zidzakhala zovuta kuzipeza koma ngati n'kotheke yesetsani kupeza zithunzi kapena zida zina zothandiza kuti ophunzira amvetse nkhaniyo. Zinthu zimene ophunzira akuziona zimathandiza kwambiri pofotokoza nkhani. Pamene n'zotheka, pezani zithunzi kuchokera ku www.freebibleimages.org (FBI) zomwe mungathe kulandira. Kumapeto kwa Buku la Mphunzitsi kuli zina zoonjezera momwe akufotokoza kwina kumene mungapeze zithunzi za nkhani za m'Baibulo mwaulere.
- Ngati mungapeze fotokope mutha kukulitsa zithunzizo, kukhala za kalala ndi kuzigwiritsa ntchito pophunzitsa.

Nthawi ya Phunziro

- **Machitidwe.** M' buku la Mphunzitsi muli machitidwe a phunziro lililonse, koma mphunzitsi ali ndi ufulu nthawi ndi nthawi kusintha machitidwe ake.
 1. Mawu Oyamba ndi kufotokoza nkhani - mphindi 15
 2. Kuphunzitsa Vesi Yoloweza – mphindi 5 mpaka 10
 3. Kutsiriza kulemba - mphindi 20
 4. Mafunso ndi zochitika zina mpindi 5 mpaka 10.

Kumbukirani mawu ofunika awa:

“Ndiuzeni ndipo ndidzayiwala,
ndionetseni ndipo ndidzakumbukira,
loleni ndichite nawo ndipo ndidzamvetsetsa.”

Zophunzitsa Nthawiyabaibulo

	KALASI 0 (sanayambe sukulu) Kalasi Yoyamba (Zaka 5-7) Kalasi Yachiwiri (Zaka 8-10)	Kalasi Yachitatu (Zaka 11-13)	Kalasi Yachinayi (Zaka 14+)
MAPHUNZIRO A	<ol style="list-style-type: none"> 1. Chilengedwe 2. Nowa 3. Petulo 4. Petulo - Mtanda 5. Abrahamu 6. Abrahamu 7. Petulo 8. Petulo 9. Yakobo 10. Akhristu Oyambirira 11. Paulo 12. Nkhani ya Khrisimasi 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Chilengedwe 2. Nowa 3. Petulo 4. Petulo - Mtanda 5. Petulo 6. Abrahamu 7. Yakobo 8. Pemphero 9. Paulo 10. Paulo 11. Paulo 12. Nkhani ya Khrisimasi 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Chilengedwe ndi Kugwa 2. Zochitika Zoyamba - Genesis 3. Petulo 4. Petulo - Mtanda 5. Petulo 6. Abrahamu 7. Yakobo 8. Moyo wa Chikhristu 9. Paulo 10. Paulo 11. Paulo 12. Nkhani ya Khrisimasi
MAPHUNZIRO B	<ol style="list-style-type: none"> 1. Moyo Woyambirira wa Khristu 2. Zodabwitsa 3. Betaniya 4. Mtanda 5. Mafanizo 6. Yosefe 7. Yosefe 8. Anthu Ankumana ndi Yesu 9. Mose 10. Mose 11. Mose 12. Nkhani ya Khrisimasi 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Mafanizo 2. Zodabwitsa 3. Betaniya 4. Mtanda 5. Akhristu Oyambirira 6. Yosefe 7. Yosefe 8. Alembi a Uthenga Wabwino 9. Mose 10. Mose 11. Mose 12. Nkhani ya Khrisimasi 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Mafanizo 2. Zodabwitsa 3. Betaniya 4. Mtanda 5. Akhristu Oyambirira 6. Yakobo ndi Banja Lake 7. Yosefe 8. Machitidwe 2:42 - Zoyenera Kuchita 9. Mose 10. Mose 11. Lamulo 12. Nkhani ya Khrisimasi
MAPHUNZIRO C	<ol style="list-style-type: none"> 1. Danieli 2. Zodabwitsa Zina Zambiri 3. Anthu Ankumana ndi Yesu 4. Imfa ya Khristu 5. Rute ndi Samuele 6. Davide 7. Davide 8. Yoswa 9. Eliya 10. Elisa 11. Yona 12. Nkhani ya Khrisimasi 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Danieli 2. Anthu Ankumana ndi Yesu 3. Zodabwitsa Zina Zambiri 4. Imfa ya Khristu 5. Rute 6. Samuele 7. Davide 8. Yoswa 9. Eliya 10. Elisa 11. Anthu Amene Mulungu Anawagwiritsa Ntchito - Chipangano Chakale 12. Nkhani ya Khrisimasi 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Danieli 2. Zoyankhula za Yesu 3. Mphamvu za Ambuye 4. Imfa ya Khristu 5. Rute 6. Samuele 7. Davide 8. Yoswa 9. Eliya 10. Elisa 11. Anthu Ena a mu Chipangano Chakale 12. Nkhani ya Khrisimasi

A1 Nkhani Yoyamba

Mulungu alenga dziko lapansi – Iyi ndi nkhani ya Mulungu kulenga kumwamba ndi dziko lapansi.

MAWU OYAMBA	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none"> • Mulungu analenga dziko lonse. • Tikuyenera kuyamika Mulungu chifukwa cha zonse zomwe analenga. <p>Ndime Yowerenga: Genesis 1:1-19 Vesi Yoloweza: Genesis 1:1</p>
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none"> • Onetsani chithunzi cha nyumba kapena funsani ana kuti ajambule nyumba. • Funsani ana mafunso a za nyumbayo – Kodi mungamange nyumba imeneyi kwa nthawi yayitali motani? Kodi mungafune chiyani kuti mumange nyumbayi? • Pamafunika zipangizo zambiri kuti mumange nyumba, koma Mulungu analenga dziko lonse popanda kugwiritsa ntchito kanthu. <ul style="list-style-type: none"> • Pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi. Mulungu asanalenge dziko kunali mdima wokhawokha. (Genesis 1:1-3) - <i>Kodi zinali zotani nthawi imeneyi pomwe kunali mdima wokhawokha? (Aphimbeni ku nkhope pofuna kuonetsa za mdima.)</i> • Tsiku loyamba Mulungu anati, “Kuyere.” Nthawi yomweyo kunayeradi. Mulungu anatchula kuyerako kuti usana ndi mdima kuti usiku. M'malo mokhala mdima nthawi zonse, panali usiku kenaka usana. (Genesis 1:4-5) • Tsiku lachiwiri Mulungu anayankhulanso ndipo analenga thambo ndi mpweya zomwe zili pamwamba pa dziko lonse lapansi. Ndipo panali madzulo ndiponso mmawa pa tsiku lachiwiri. (Genesis 1:6-8) - <i>Uzani ana kuti apumire m'mkati kwambiri. Fotokozani kufunika kwa mpweya umene watizungulira.</i> • Mpaka nthawi imeneyi, dziko lapansi linali lokutidwa ndi madzi ndipo tsopano inali nthawi yoti alenge mtunda. • Mulungu anayankhula ndipo madzi anasuntha kenaka mtunda unaoneka. Madzi amene anzungulira mtunda anatchedwa nyanja. Kenaka Mulungu anayankhulanso, “Mtunda udzaze ndi zomera zonse ndi mitengo.” Mulungu ataona zonse zimene analenga anati zinali bwino. Ili linali tsiku lachitatu. (Genesis 1:9-13) - <i>Funsani ana kuti atchule mbewu zimene zimamera m'dera lawo. Yankhulani za mitundu yosiyanasiyana, maonekedwe ndi misinkhu yake ndiponso za kufunika kwa zomerao ndi kukongola kwake.</i> • Tsiku lachinayi Mulungu analenga zowunikira zapadera mlengalenga – dzuwa lidziwunikira usana ndipo mwezi ndi nyenyezi usiku. Mulungu anaona zowunikira zomwe analenga zinali bwino. (Genesis 1:14-19) - <i>Yankhulani za ubwino wa dzuwa. Khalani ndi chidwi chifukwa cha kuchuluka kwa nyenyezi!</i> • <i>Fotokozerani ana kuti Mulungu analenga dziko lokongola kwambiri momwe muli chilichonse chimene tingachifune ndipo tikuyenera kumuyamika lye.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Mulungu alenga dziko lapansi/Mulungu alenga dziko lonse</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza - Genesis 1:1.</p>
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none"> • Kodi moyo unali wotani Mulungu asanalenge dziko? • Kodi chinthu choyamba chomwe Mulungu analenga ndi chiyani? • Tsiku 2 Mulungu analenga thambo ndi _____. • Pachiyambi, kodi dziko lapansi linali lotani? • Tsiku 3, kodi zomera ziwiri ziti zomwe Mulungu analenga? • Kodi Mulungu analenga chiyani chowunikira usana? • Kodi Mulungu analenga chiyani zowunikira usiku? • Tsirizani vesiyi – “Pachiyambi Mulungu analenga...”

A1 Nkhani Yachiwiri

Mulungu analenga nyama ndi anthu – Iyi ndi nkhani ya zamoyo zonse zimene Mulungu analenga.

	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Mulungu analenga anthu m'chifanizo chake ndipo ndi apadera kwambiri kwa Iye.• Ife tikuyenera kutsatira Njira za Mulungu chifukwa ndi Iye amene anatilenga. <p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 1:20-2:3</i> Vesi Yoloweza: <i>Genesis 1:31</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Bweretsani chinthu chomwe mwapanga chomwe sichinapangidwe bwino, monga keke yopserera. Fotokozani za kukhumudwa kumene kumabwera ngati zinthu sizinayende monga mmene timayembekezera.• Fotokozerani ana kuti Mulungu analenga zamoyo zosiyanasiyana ndipo Iye sanakhumudwe pamene anzilenga.• KAPENA - Ana achite sewero lomwe akhale ngati nyama. Ili likhale sewero longoliganiza pomwepo.
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Tsiku lachisanu Mulungu analenga miyandamiyanda ya mbalame zosiyanasiyana ndi nsomba. Mulungu ataona zonse zimene analenga ananena kuti “Zili bwino.” (Genesis 1:20-23) - <i>Kambiranani za mbalame/nsomba zochepe chabe m'magulu anu.</i>• Tsiku lachisanu ndi chimodzi Mulungu analenga nyama zonse. Iye analenga nswala ya khosi lalitali ndiponso mikango ndi akambuku okhala ndi mano akuthwa – Mulungu ndiye amene analenga zonsezi! (Genesis 1:24-25)• Ngakhale Mulungu analenga zinthu zambiri zodabwitsa, Iye ankayeneranso kulenga chinthu china chapadera kwambiri ndipo anachilenga mwapadera kwambiri. <i>Onetsani ana dongo lochepe m'manja mwanu ndipo afunseni chomwe mungapange kuchokera ku dongo limenelo.</i> Mulungu anatenga dongo ndipo anapanga munthu woyamba kuchokera ku dongo limenelo. Munthuyo anakhala wamoyo pamene Mulungu anapumira mpweya wake mwa Iye. Dzina la munthu woyambayayu ndi Adamu. (Genesis 1:26-31) <i>Fotokozerani ana kuti pamene Mulungu anakalenga munthu anagwiritsa ntchito chifanizo chake (chomwe Iye ali) ngati chitsanzo. Izi zikutanthauza kuti Mulungu anakonza kuti munthu akhale wofanana naye mu njira zina. Pakuti ife tinalengedwa m'chifanizo cha Mulungu, ndife osiyana kwambiri ndi zamoyo zina zonse. Kambiranani za zolengedwa. Izi zikutanthauza kuti ife timazindikira kusiyana kwa chabwino ndi choyipa, ndipo titha kuphunzira kutsatira Mulungu ndi njira zake.</i>• Mulungu analenga dziko lapansi ndi zonse zili m'menemo pa masiku asanu ndi limodzi. Iye atatsiriza kulenga ananena kuti zinali bwino. Tsiku lachisanu ndi chiwiri Iye anapuma ndi kuyamikira zonse zomwe anzilenga. (Genesis 2:1-3) - <i>Kambiranani za kufunika kopuma pamene tagwira ntchito.</i>• Tsirizani ponena kuti dziko limene Mulungu analenga linali labwino kwambiri ndipo Iye anali wosangalala ndi chilichonse chimene anachilenga. <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Mulungu analenga nyama ndi anthu/Mulungu analenga dziko lapansi ndi munthu.</p>
PHUNZIRANI	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza - Genesis 1:31.
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Kodi ndi tsiku liti lomwe Mulungu analenga mbalame ndi nsomba?• Kodi Mulungu anati chiyani za zimenezi?• Kodi Mulungu analenga chiyani pa tsiku lachisanu ndi chimodzi pamodzi ndi nyama?• Kodi Mulungu anati chiyani atalenga zinthu zonse?• Kodi munthu woyamba anali ndani?• Kodi Mulungu anagwiritsa ntchito chiyani pomulenga?• Kodi Mulungu analenga dziko lapansi masiku angati?• Kodi Mulungu anachita chiyani pa tsiku lachisanu ndi chiwiri?

A1 Nkhani Yachitatu

Mwamuna ndi mkazi woyamba – Iyi ndi nkhani ya Adamu ndi Hava.

	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Mulungu anamupangira Adamu mkazi, kuti azimuthandiza kusamalira chilengedwe.• Mulungu akulamulira zinthu zonse. <p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 2:4-25</i> Vesi Yoloweza: <i>Genesis 2:18 kapena Salimo 24:1</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Ngati anawo amawudziwa munda, kambiranani zomwe iwo anaona zikumera m'menemo, kapena onetsani maluwa/chipatso/ndiwo za masamba zomwe zimapezeka kwanuko. Ngati anawo sakuudziwa munda, fotokozani kuti ndi malo amene anthu amadzalamo zinthu ndipo fotokozani momveka bwino.• Fotokozani kuti Munda wa Edeni unali wokongola kwambiri kuposa china chilichonse tingajambule kapena kuganizira.• Kambiranani za Munda wa Edeni – Kodi inu mukanakonda mukukhala m'Munda wa Edeni? Kodi mukuganiza kuti chikanakusangalatsani kwambiri m'Mundamo chikanakhala chiyani? Kodi mukuganiza kuti Adamu ankasowa wocheza naye m'Mundamo?
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Adamu ankakhala m'munda wokongola wotchedwa Edeni. M'menemo, Mulungu anamupatsa chilichonse chimene akanachifuna – chakudya ndi madzi. Mulungu anawuzanso Adamu kuti azisamalira mundawo. (<i>Genesis 2:15</i>)• Mulungu anaonetsa Adamu za moyo zonse zimene lye analenga. Adamu anazipatsa mayina zamoyo zonse. (<i>Genesis 2:19-20</i>)• Mulungu sanafune kuti Adamu akhale yekha. Adamu anali pakati pa nyama zokongola kwambiri, mbalame, mitengo ndi zomera koma Mulungu anadziwa kuti iye ankafuna wina wapadera woti aziyanjana naye m'mundamo. Mulungu anagoneka Adamu tulo ndipo ali chigonere, lye anapanga mkazi woyamba kuchokera ku nthiti ya Adamu. Adamu sanalinso yekha. lye anali ndi mkazi amene anamutcha Hava amene anakhala mnzake wosamalira naye munda umene Mulungu anamupatsa uja. (<i>Genesis 2:20-24</i>)• M'mundamo munali mitengo yambiri. Pakati pa munda panali mtengo wotchedwa “Mtengo Wodziwitsa Chabwino ndi Choyipa”. Mulungu anawuza Adamu ndi Hava kuti atha kudya zipatso za mitengo yonse m'mundamo kupatula “Mtengo Wodziwitsa Chabwino ndi Choyipa”. (<i>Genesis 2:16-17</i>) - <i>Yankhulani za malamulo amene ana amapatsidwa ku nyumba zawo kapena ku sukulu. N'chifukwa chiyani timayenera kukhala ndi malamulo? (Kuti titetezedwe ndi kusangalala.) Onetsani ngati ana amvetsa za lamulo limene Mulungu anapereka kwa Adamu ndi Hava kuti amvere.</i>• <i>Fotokozani kuti Mulungu analenga dziko lokhala ndi malamulo ake, choncho lye ndiye ali ndi udindo wosankha momwe anthu akuyenera kukhalalira. Ifenso tikuyenera kumvera malamulo ake.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Mwamuna ndi mkazi woyamba/Mwamuna woyamba ndi mkazi woyamba.</p>
PHUNZIRANI	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza - <i>Genesis 2:18 kapena Salimo 24:1</i> .
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Kodi Adamu ankakhala kuti?• Kodi Adamu anali ndi ntchito yotani m'mundamo?• Kodi mayina a nyama anachokera kuti?• Tsirizani chiganizo ichi: Mulungu anafuna kumapangira Adamu m_____.• Kodi Mulungu anagwiritsa ntchito chiyani popanga mkazi wa Adamu?• Kodi mkazi wa Adamu dzina lake anali ndani?• Tchulani dzina la mtengo wapadera m'mundamo.• Kodi lamulo la Mulungu pa “Mtengo Wodziwitsa Chabwino ndi Choyipa” linali loti chiyani?

A1 Nkhani Yachinayi

Dziko la Mulungu lawonongedwa – Iyi ndi nkhani ya kubwera kwa tchimo m'dziko lapansi.

	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Adamu ndi Hava sanamvere Mulungu ndipo anaononga chilengedwe chake chabwino.• Ifenso sitimvera Mulungu ndipo tikuyenera kumva chisoni chifukwa cha machimo athu ndi kupempha Mulungu kuti atikhululukire. <p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 3:1-24</i> Vesi Yoloweza: <i>Aroma 5:1 kapena Aroma 5:12</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Bweretsani chithunzi chokongola ndipo muchiononge polembalembapo kapena kung'amba.• Kambiranani za chithunzichi - Kodi mwachita chiyani ndi chithunzicho? Nanga tsopano chikuoneka motani?• Fotokozani kuti Mulungu analenga dziko labwino kwambiri koma kenaka linaonongedwa.
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Pamene dziko linalengedwa, chilichonse chinali chabwino kwambiri koma tsiku lina mdani wa Mulungu, Satana, anabwera ngati njoka m'mundamo. Njokayo inayankhula ndi Hava ndipo inamuwaza kuti adye chipatso cha "Mtengo Wodziwitsa Chabwino ndi Choyipa". Akadya adzakhala wanzeru ngati Mulungu. (Genesis 3:1-5)• Hava anamvera mdani wa Mulungu. Iye sanamvere Mulungu ndipo anathyola zipatsozo. Iye anakapereka kwa Adamu ndipo onse awiri anadya. (Genesis 3:6)• Nthawi ya madzulo Mulungu anafuna kuyankhula ndi Adamu ndi Hava koma lwo anadziwa kuti sanamvere Mulungu ndipo anabisala. (Genesis 3:7-8) - <i>Kodi ilipo nthawi imene simunamvere wina wake? Kodi chilipo chomwe chinachitika chifukwa cha kusamverako? Fotokozani kuti Adamu ndi Hava sakanatha kubisala pamaso pa Mulungu ngakhale ife sitingathe.</i>• Mulungu anayitana "Kodi uli kuti?" Iye anakadziwa kuti sanamumvere ndipo ngakhale ankawakonda, ankayenera kulangidwa chifukwa cha kusamvera kwawo. Mulungu anatulutsa Adamu ndi Hava m'munda wa Edeni. Tchimo lawo linaononga chilengedwe cha Mulungu ndi ubale wawo ndi Mulungu. Chifukwa cha machimo a Adamu ndi Hava, minga ndi nthula zinayamba kumera. Nyama ndi anthu anayamba kudwala ndipo choopsa kwambiri, imfa inalowa m'dziko lapansi. (Genesis 3:9-24)• <i>Mulungu amakhumudwa pamene tachita zinthu zolakwika. Kambiranani zinthu zomwe ana amachita zomwe sizikondweretsa Mulungu. Ngakhale ife timatero, Mulungu amatikonda kwambiri. Mwana wa Mulungu, Yesu, anafa pa mtanda kuti tikhululukidwe machimo athu ndi kukhala abwenzi a Mulungu pamene tamukhulupirira.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Dziko la Mulungu lawonongedwa/Kuonongeka kwa dziko la Mulungu.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – Aroma 5:1 kapena Aroma 5:12.</p>
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Kodi ndi ndani amene ananamiza Hava kuti adye chipatso?• Kodi Satana anamukakamiza motani Hava kuti adye chipatso?• Kodi Hava anakapatsa ndani chipatso?• Kodi Adamu ndi Hava anachita chiyani pamene Mulungu anawayitana?• Kodi Mulungu anamva bwanji mu mtima chifukwa cha zimene anachita Adamu ndi Hava?• Kodi chinachitika kwa Adamu ndi Hava ndi chiyani?• Kodi Mulungu amamva bwanji mu mtima ife tikachita zinthu zolakwika?• Kodi tingakhululukidwe bwanji zoyipa zomwe timachita?

A2 Nkhani Yoyamba

Nowa amvera Mulungu – Iyi ndi nkhani ya Nowa kupanga Chombo.

	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Nowa ndi banja lake pamodzi ndi nyama anapulumuka mu Chombo.• Mulungu anapereka njira yathu yoti tipulumukirenso, choncho tikuyenera kumukhulupirira monga Nowa. <p>Ndime Yowerenga: Genesis 6:5-22 Vesi Yoloweza: Machitidwe 16:31</p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Funsani ana kuti akuwuzeni nyama zimene amazikonda kwambiri.• Kambiranani zomwe zingachitike ngati nyama zonsezo zitakhala malo amodzi! Kodi zingakwane pa malo otani? Kodi phokoso lake lingakhale lotani? Nanga pangakhale fungo lotani pamenepo?• Fotokozani kuti aphunzira nkhani yochokera m'Baibulo ya nthawi imene anthu ena ndi nyama zambiri analowa mu bwato lalikulu kwambiri.
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Pamene Mulungu analenga dziko lathu, zinthu zonse zinali bwino ndipo zinali zokongola. Pasanathe nthawi yayitali, Adamu ndi Hava sanamvere Mulungu. Ana awo anasanduka odzikonda ndi woyipa ndipo Mulungu anamva chisoni chifukwa analenga iwo. (Genesis 6:5-6)• Anthu onse a dziko lapansi anali oyipa kwambiri, koma panali munthu mmodzi amene anakondweretsa Mulungu! Dzina lake anali Nowa. Munthu ameneyu ndi mkazi wake pamodzi ndi ana ake aamuna atatu ankayesetsa kuchita zinthu zimene Mulungu ankafuna, pamene mabanja ena onse amene anawazungulira ankachita zowakondweretsa okha ndipo anayiwala zonse za Mulungu. (Genesis 6:8-10)• Mulungu anaganiza zoti alange dziko lonse chifukwa cha kuyipa kwa anthuwo. Iye anafuna kuti Nowa apange bwato lalikulu lotchedwa Chombo. Akadzatsiriza kumanga, Mulungu adzatumiza madzi achigumula pa dziko lapansi. Chamoyo chilichonse chidzafa, koma Nowa ndi banja lake adzapulumuka mu Chombo. (Genesis 6:13-18)• Nowa anachita chilichonse monga mmene Mulungu anamuwuzira. Mwina ntchito yomanga bwato lalikulu lotchedwa Chombo inatenga zake zana limodzi. <i>Fotokozani za kukula kwake - kukula ngati bwalo la mpira kapena nyumba zitatu zosanjikana.</i> Pamapeto pake, atagwira ntchito yotopetsa, anatsiriza kumanga Chombo. (Genesis 6:22)• Mulungu anawuza Nowa kuti alowetse m'Chombo nyama ndi mbalame za mitundu yonse. <i>Tchulani mayina a nyama zina zomwe ana azitchula poyamba paja.</i> Nyama zimenezi pamodzi ndi Nowa ndi banja lake anapulumuka m'Chombomo. <i>Werengani mpaka kasanu ndi katatu za anthu a banja la Nowa amene analowa m'Chombo.</i> Pamene onse analowa, Mulungu anatseka khomo. Chikonzero chake chowapulumutsa chinakwaniritsidwa. (Genesis 7:13-16)• <i>Fotokozani kuti nafenso timachita zinthu zambiri zolakwika. Ife tikuyenera kupulumutsidwa ku chilango cha tchimo lathu. Mulungu anapereka njira yoti ife tipulumukire pamene takhulupirira Mwana wake, Ambuye Yesu. Iye ali ngati Chombo chathu chimene Mulungu anatipangira.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Nowa amvera Mulungu.</p>
PHUNZIRANI	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – Machitidwe 16:31.
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Kodi vuto pa dziko lapansi ndi chiyani?• Kodi Mulungu anaganiza kuti achite chiyani?• Kodi ndi ndani amene anakondweretsa Mulungu?• Kodi Mulungu anawuza Nowa kuti achite chiyani?• Kodi analowa mu Chombo ndi ndani?• Kodi ndani anatseka khomo la Chombo?• N'chifukwa chiyani anthu amene anali m'Chombo anapulumuka?• Kodi ife tingapulumuke bwanji ku chilango cha machimo athu?

A2 Nkhani Yachiwiri

Kupulumuka m'Chombo – Iyi ndi nkhani ya nthawi imene chigumula chinayamba.

	<p>Ife tikuphuzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Nowa ndi banja lake anatetezedwa m'Chombo chifukwa anadalira ndi kumvera Mulungu.• Mulungu analonjeza kuwateteza akamudalira Iye. <p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 7:1-24</i> Vesi Yoloweza: <i>Miyambo 29:25b</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Funsani ana kuti akufotokozereni chimene anamanga kapena kupanga – Kodi anagwiritsa ntchito chiyani popanga chimenecho? Kodi chinali chovuta kupanga? Kodi alipo amene anakuthandizani?• Onaninso nkhani ya m'mbuyo - Kodi Nowa anagwiritsa ntchito chiyani popanga Chombo? Kodi mukuganiza kuti chinali chovuta kumanga? Kodi anachimanga chifukwa chiyani?• Tsindikani kuti ngakhale inali ntchito yovuta, Nowa anamanga Chombo chifukwa Mulungu anamuwuzwa kuti atero. Iye anamvera malangizo a Mulungu kwathunthu.
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Tsopano Nowa ndi banja lake anali mu Chombo. (Genesis 7:6-7)• Patatha masiku asanu ndi awiri mvula inayamba kugwa, ndipo inapitirira kubwera tsiku ndi tsiku! Udzu wonse ndi maluwa zinamizidwa ndi madzi. Mitsinje ndi nyanja zinasefukira kwambiri. (Genesis 7:17-20) - <i>Fotokozani kuti tsopano nthawi inali itatha kwa anthu amene ankamuseka Nowa aja ndipo anali kunjwa kwa Chombo.</i>• Madzi anapitirira kuchuluka kwambiri. Madziwo anamiza nyumba, mitengo ngakhalenso mapiri ataliatali. (Genesis 7:20 -21) - <i>Taganizani, kodi Nowa ndi banja lake ankamva chiyani m'mitima mwawo pamene anali mu Chombo? Kodi chikanachitika ndi chiyani ngati Nowa akanapanda kumvera Mulungu?</i>• M'mkati mwa Chombo, Nowa ndi banja lake pamodzi ndi nyama zonse anali atapulumuka! Chifukwa Nowa anadalira ndi kumvera Mulungu, iye anatetezedwa ku chilango chimenechi. (Genesis 7:23)• <i>Fotokozani kwa ana kuti Mulungu akufuna kuti ife tizimumvera ndi kumudalira. Mulungu walonjeza kutiteteza ngati tingamudalire ndi kumumvera monga anachitira Nowa.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Kupulumuka m'Chombo/Kutetezedwa m'Chombo.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – Miyambo 29:25b.</p>
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Kodi Nowa anaonetsa motani kuti ankakhulupirira Mulungu?• Ndi ndani analowa mu Chombo pamodzi ndi Nowa?• Kodi anakhala nthawi yayitali yotani mu Chombo mvula isanayambe kugwa?• Kodi madzi anachuluka motani?• Kodi ndi ndani amene anatetezedwa?• N'chifukwa chiyani Nowa anatetezedwa?• Kodi ndi ndani amene angatiteteze ngati titamukhulupirira?

A2 Nkhani Yachitatu

Kuyamba mwatsopano – Iyi ndi nkhani ya nthawi imene chigumula chitatha.

	<p>Ife tikuphonzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Mulungu anapereka mwayi kwa Nowa ndi banja lake oyambanso mwatsopano, m'dziko latsopano lokhalamo.• Mulungu angathe kuyetsa miyoyo yathu ndi kuyipanga kukhala yatsopano ngati titamupempha kuti atikhululukire. <p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 8:1-19</i> Vesi Yoloweza: <i>2 Akorinto 5:17</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Awuzeni ana kuti Nowa ndi banja lake anakhala nthawi yayitali mu Chombo muja.• Lolani ana aganizire momwe zinalili pokhala mu Chombo - Kodi inu mukanamachitamo chiyani tsiku lonse? Kodi inu mukuganiza mukanamamva chiyani mu mtima mwanu nthawi imeneyi?
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Patatha masiku makumi anayi mvula inasiya kubwera. Koma madzi anali ataphimba mapiri onse. (Genesis 8:1-4)• Tsiku lina Nowa anatuma khwangwala kuchokera mu Chombo kuti akaone ngati madzi aphwa koma khwangwala sanabwererense. Kenaka anatuma nkunda imene inabwerera msanga. Patatha sabata anayitumanso ndipo aliyense anali osangalala pamene inabwerera ili ndi nthambi ya olivi ku kamwa kwake. <i>Fotokozani kuti izi zikutanthauza kuti msonga za mitengo zinayamba kuoneka pamwamba pa madzi. (Genesis 8:6-11)</i>• Patapita masiku asanu ndi awiri, Nowa anatumanso nkunda ija. Nthawi imeneyi sinabwererense. Nowa anazindikira kuti madzi aphwa kwambiri ndipo nkunda yapeza malo wokhalapo atsopano. Kumapeto kwake, Chombo chija chinayima pa phiri lalitali lotchedwa Ararati. (Genesis 8:4)• Pamene nthaka inawuma, Mulungu anawuza Nowa kuti atuluke mu Chombo pamodzi ndi nyama zonse. Iyi inalitu nkhani yabwino kwambiri kwa aliyense! Iwo anali atasekeredwa mu Chombo nthawi yayitali! <i>Kodi inu mukuganiza kuti Nowa ndi banja lake anamva bwanji m'mitima mwawo pamene anatuluka mu Chombo? Funsani ana kuti afotokoze kuti dziko latsopanoli linali lotani. (Genesis 8:15-19)</i>• <i>Fotokozani kuti ife lero si anthu osiyana ndi anthu a nthawi ya Nowa. Mulungu akhoza kuchotsa zoyipa miyoyo yathu ndi kutipatsa mitima yoyera ndi yatsopano. Tikuyenera kupempha Mulungu kuti atikhululukire ndi kudalira Ambuye Yesu amene anafa pa mtanda kuchotsa machimo athu.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Kuyamba mwatsopano.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – 2 Akorinto 5:17. <i>Fotokozani kuti Ambuye Yesu angathe kusintha miyoyo yathu m'kati.</i></p>
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Kodi ndi mbalame iti yomwe Nowa anayituma koyamba kuchokera mu Chombo?• Kodi nkunda inabweretsa chiyani m'kamwa mwake nthawi yachiwiri?• Kodi Chombo chinayima pati?• Kodi ndi ndani amene anamuwuzwa Nowa kuti atuluke mu Chombo? Kodi ndi ndani amene anapulumuka ku chigumula?• Kodi ndi ndani amene analangidwa chifukwa cha machimo athu?• Kodi tikuyenera kuchita chiyani ndi mtima woyera?• Tsirizani mawu amene palibe: “Ngati munthu aliyense ali mwa Khristu, iye ndi _____.

A2 Nkhani Yachinayi

Lonjezo la Mulungu – Iyi ndi nkhani ya Nowa kuyamika Mulungu.

	<p>Ife tikuphonzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Mulungu amasunga malonjezo ake nthawi zonse.• Monga mmene Mulungu anasamalira Nowa ndi banja lake, Mulungu analonjeza kuti sadzawasiya amene amamukhulupirira ndi kumutsatira. <p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 8:20-22; 9:8-17</i> Vesi Yoloweza: <i>Ahebri 13:5</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Perekani chitsanzo kwa ana za nthawi imene munthu wina anakulonjezani.• Perekani mpata kwa mwana kuti afotokozere mnzake za nthawi imene wina anamulonjeza.• Funsani ana ngati alipo wina aliyense amene sanakwaniritse lonjezo lake kwa iwo.• Fotokozerani ana kuti Baibulo ndi lodzaza ndi malonjezo a Mulungu ndi kuti iye salephera kukwaniritsa malonjezo akewo.• Uzani ana kuti ngati tasankha kudalira Mulungu ndi kumutsatira, Iye walonjeza kuti sadzatisiya.
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Nowa ndi banja lake anatetezedwa! Iwo anakhala mu Chombo nthawi yayitali, koma tsopano Mulungu akuti Nowa ndi banja lake pamodzi ndi nyama zonse atuluke mu Chombo. (Genesis 8:15-19)• Chinthu choyamba chomwe Nowa anafuna kuchita ndi kunena “Zikomo” kwa Mulungu chifukwa chomusunga iye pamodzi ndi banja lake nthawi ya madzi a chigumula! Iye anachita izi potola miyala yayikulu ndi kuwunjika kumanga guwa lansembe. Mu nthawi ya Nowa anthu ankapereka nsembe pa guwa yoyamika Mulungu chifukwa cha zonse zomwe wawachitira. (Genesis 8:20-21) - <i>Kodi ndi ziti zomwe ife tinganene zikomo kwa Mulungu? (Lembani zimenezo pa bolodi kapena pa pepala lalikulu.)</i>• Mulungu anakondwera kwambiri ndi Nowa pamodzi ndi banja lake chifukwa anakumbukira kuyamika. Ndipo Iye anawalonjeza zabwino kwambiri ponena kuti, “Ine sindidzaononga dziko lonse lapansi ndi madzi.” (Genesis 8:21-22)• Kenaka Mulungu anawaonetsa chizindikiro chomwe chikhale chikumbutso cha lonjezo lake. Ichi ndi utawaleza. Nthawi ina iliyonse Nowa ndi banja lake akaona utawaleza anakumbukira za lonjezo la Mulungu. (Genesis 9:12-13) - <i>Fotokozani mitundu imene ili mu utawaleza ndi kukongola kwake. Limbikitsani ana kuti azilingalira za Mulungu ndi malonjezo ake nthawi zonse akaona utawaleza.</i>• <i>Kodi Mulungu anasunga lonjezo limene anachita kwa Nowa? Thandizani ana kuti amvetse kuti Mulungu amasunga lonjezo lake lokhala ndi ife pamene tamukhulupirira. (Onani Vesi Yoloweza.)</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Lonjezo la Mulungu.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – Ahebri 13:5.</p>
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Sankhani mafunso kuchokera pa zomwe mwaphonzira m’mbuyomu za Nowa kuti muone zomwe ana akukumbukira.• Bwerezani Vesi Yoloweza yomwe ana aphonzira pamene amamva nkhani ya Nowa.• Ana ajambule chithunzi za chomwe chawasangalatsa pa nkhanayi/kapena alembe chiganizo cha zomwe iwo aphonzira.• Gulu kapena kalasi lijambule anthu ndi nyama akutuluka mu Chombo, komanso guwa lansembe ndi utawaleza.

A3 Nkhani Yoyamba

Yesu ayitana Petulo – Iyi ndi nkhani ya kutsatira Yesu.

	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Yesu anafuna anthu ena oti azigwira nawo ntchito komanso amene adzapitiriza ntchito yake m'tsogolo.• Kuti tikhale ogwira naye ntchito, tikuyenera kutsatira Yesu ndi kumumvera. <p>Ndime Yowerenga: <i>Mateyu 4:18-22</i> Vesi Yoloweza: <i>Mateyu 4:19</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Fotokozani za anzanu. Kodi anawa anakumana nawo kuti anzawo? N'chifukwa chiyani kuli kofunika kukhala ndi anzathu? Kodi ndi abwenzi ati abwino amene tikuyenera kukhala nawo? (Iwo akhale achifundo, othandiza ndi odalirika...)• Fotokozani kuti Ambuye Yesu anali ndi abwenzi abwino ndipo lero tiphunzira za ena mwa abwenzi amenewa.• Malo ochitikira – nyanja yayikulu yotchedwa Galileya yozunguliridwa ndi mapiri. Asodzi akugwira nsomba. Fotokozani zomwe ankagwiritsa ntchito pogwira nsomba (mabwato, maukonde ndi zina zambiri). Inali ntchito yolemetsa kwambiri!
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Yesu akuyitana Petulo ndi m'bale wake Andreya: (<i>Mateyu 4:18-19</i>) Petulo ndi Yohane anali atakumana kale ndi Ambuye Yesu ndipo anazindikira kuti anali wofunika kwambiri. Tsopano Yesu akufuna kuti iwo asiye kupha nsomba ndipo amutsatire ndi kugwira naye ntchito! <i>Gwiritsani ntchito mawu enieni amene Yesu anayankhula ndipo fotokozani kuti ntchito yawo yatsopano idzabweretsa anthu ena kwa Yesu. Taonani iyi inali ntchito yopambana kwambiri imene Yesu wawayitana kuti agwire!</i>• Yankho la Petulo ndi Andreya: (<i>Mateyu 4:20</i>) Iwo anazindikira nthawi yomweyo kuti izi zinali zoyenera kuti achite. Iwo anaonetsa kufuna kwawo potsatira Yesu nthawi yomweyo. <i>Fananizani ndi zomwe ana amachita m'miyoyo yawo ya kumvera mofulumira. Kambiranani za chisangalalo cha Petulo ndi Andreya pamene anawuzidwa zimenezi (akondwa ndipo akusangalala chifukwa Yesu wawasankha). Kwa ana a Kalasi Yachiwiri fotokozani kuti tsopano amenewa ndi ophunzira a Yesu. Izi zikutanthauza kuti anali okonzeka kutsatira Yesu kulikonse kumene akupita, kuphunzira ndi kumumvera.</i>• Yesu ayitana Yakobo ndi Yohane: (<i>Mateyu 4:21, 22</i>) Nthawi ina tsiku lomwelo, Yesu anayitani asodzi ena awiri ndipo nawonso anamutsatira.• <i>Ambuye Yesu akufuna aliyense wa ife kuti akhale womutsatira wake. Ngati ndife otsatira ake adzatituma tigwire ntchito yake. Monga asodzi a nkhani yathu ya m'Baibulo, ife tikuyenera kumvera mawu ake. Kodi ndi kuti komwe anatilemba mawu ake? Fotokozani kufunika kwa Baibulo.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Yesu ayitana Petulo.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani Vesi Yoloweza, onani ngati ana akumvetsa mawu akuti “asodzi a anthu”– <i>Mateyu 4:19</i>.</p>
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Kodi Yesu anayitana asodzi angati?• Kodi iwo ankagwira ntchito yawo kuti?• Kodi m'bale wa Andreya anali ndani?• Kodi Yesu anawalonjeza kuti adzakhala chiyani?• Kodi Petulo ndi Andreya anasiya chiyani pamene ankapita ndi Yesu?• Kodi Petulo ndi Andreya anachita chiyani pofuna kuonetsa kuti analidi ophunzira a Yesu?• Kodi abale ena awiri amene Yesu anawapezanso ndi ati?• Kodi Yakobo ndi Yohane ankachita chiyani pamene Yesu ankawapeza?• Kodi iwo anali ndi yani m'bwato mwawo?• Tsirizani chiganizochi – ngati tikufuna kukhala otsatira a Yesu tikuyenera _____ mawu ake.

A3 Nkhani Yachiwiri

Yesu athandiza Petulo – Iyi ndi nkhani ya Petulo kuzindikira kuti ndi wochimwa.

	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Mphamvu za Yesu zinasintha moyo wa Petulo.• Yesu ndi Mwana wa Mulungu ndipo Iye akufuna kuti timutsatire monga anachitira Petulo. <p>Ndime Yowerenga: <i>Luke 5:1-11</i> Vesi Yoloweza: <i>Luka 5:10</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Funsani ana kuti afotokoze zomwe amatha kuchita bwino. Kumbutsani ana kuti tonse tili ndi maluso ndi kuthekera kochita zinthu.• Petulo ankadziwa bwino kupha nsomba. Iye anali msodzi kwa nthawi yayitali. Koma mu nkhani ya lero, Petulo akuphunzira kuti akuyenera kumvera malangizo a Yesu kuti achite bwino! (Fotokozani kuti nthawi zina Petulo amatchedwanso Simoni kapena Simoni Petulo.)
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Kumbutsani ana zomwe zinachitika m'phunziro lapita. Mu nkhani yathu lero, Yesu akugwiritsa ntchito bwato la Petulo kuphunzitsa anthu Mawu a Mulungu. (Luka 5:1-3)• Yesu alamula Petulo: Yesu akuwuzza Petulo kuti aponye khoka kwa kuya kuti agwire nsomba. (Luka 5:4-5) - <i>Kambiranani za momwe Petulo ankamvera mu mtima mwake.</i>• Apha nsomba zambiri: (Luka 5:6-7) - <i>Fotokozani kusiyana kwa nsomba zomwe anapha usiku umenewu ndi usiku winawo.</i> Ichi chinali chodabwitsa! Mlengi wa nsomba anali pamodzi ndi Petulo m'bwato ndipo inali mphamvu yake yomwe inabweretsa nsomba mu ukonde wa Petulo.• Zochita za Petulo: (Luka 5:8-9) Fotokozani kuti Petulo anadziwa Yesu chomwe anali mwatsopano. Iye sanali munthu wamba monga Petulo. Iye anali Ambuye Yesu wamphamvuzonse wosafanana ndi iye, Petulo anazindikira kuchimwa kwake.• Ntchito yatsopano ya Petulo: (Luka 5:10) Yesu anawuzza Petulo kuti kuyambira nthawi imeneyi adzakhala msodzi wa anthu! <i>Fufuzani ngati ana akumvetsa za nkhani imeneyi kuchokera m'phunziro la sabata yatha.</i> Tsopano Petulo anazindikira kuti Ambuye Yesu anali ndi ntchito yapadera yoti agwire choncho anasiya zonse ndi kuyamba kutsatira Yesu. (Luka 5:11)• <i>Ambuye Yesu akufuna ife kuti tizindikire mphamvu yake yayikulu. Ife titha kukhala naye m'miyoyo yathu. Iye amabweretsa kusintha kwakukulu pamene tasankha kumumvera ndi kumutsatira monga anachitira Petulo.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Yesu athandiza Petulo.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – Luka 5:10.</p>
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Kodi Yesu anagwiritsa ntchito chiyani chomwe chinali cha Petulo?• Kodi Yesu anawuzza Petulo achite chiyani atatsiriza kuyankhula ndi gulu la anthu?• Kodi ndi liti lomwe Petulo ankafuna kupha nsomba?• Kodi Petulo anachita chiyani atagwira nsomba zambiri?• Kodi timatcha chiyani chomwe Yesu amachita chifukwa ndi Mwana wa Mulungu?• N'chifukwa chiyani Petulo anagwa pansu pa mapazi a Yesu?• Kodi wina ndi ndani amene anadabwa kwambiri ndi nsomba zambiri zomwe anagwirazo?• Kodi Yesu anamuwuzza Petulo kuti kuyambira nthawi imeneyi azichita chiyani?• Kodi kumapeto kwa nkhanayi Petulo ndi anzake aja anachita chiyani? <p>Onetsani: Ngati mukuphunzitsa ngati sukulu pamene pali zolemba, mapepala ndi sizasi, mwana aliyense ajambule nsomba ndi kudula. Nsomba zonse muzionetse pamodzi kuti mukumbutse ana nkhanayi. Mwachitsanzo, Ambuye Yesu anathandiza Petulo kuti agwire nsomba zambiri.</p>

A3 Nkhani Yachitatu

Yesu aletsa mphepo yamphamvu – Iyi ndi nkhani ya mphamvu za Yesu.

	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Yesu anali ndi mphamvu zoletsa namondwe chifukwa lye ndi Mwana wa Mulungu.• Ife tikuyenera kukhulupirira kuti Ambuye Yesu ndi Mwana wa Mulungu. <p>Ndime Yowerenga: <i>Mateyu 8:23-27</i> Vesi Yoloweza: <i>Mateyu 8:27</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Fotokozani za nyengo molingana ndi zomwe anawo akudziwa. Kodi nyengo imasintha mofulumira kwambiri? Mwachitsanzo: Kodi mvula yamphamvu imabwera mwadzidzidzi?• Fotokozani za nyengo imene imakhudza anthu amene akuyenda pa nyanja ndi momwe mphepo imachitira. Mu nkhani yathu ya lero Yesu ndi ophunzira ake akuwoloka nyanja ya Galileya.
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Kuyamba mwabata: Fotokozani tanthauzo la mawu akuti bata – mosachedwa Yesu anagona tulo. (<i>Mateyu 8:23-24</i>)• Namondwe: Mwadzidzidzi kunayamba namondwe owopsa kwambiri ndipo ophunzira anachita mantha. (<i>Mateyu 8:24</i>) Fotokozani zomwe zinkachitika – phokoso, kulowa kwa madzi m'bwato, kuyesetsa kuchotsa madzi m'bwato...• Mantha a ophunzira: <i>Fotokozani kuti iwo anali ndi mantha aakulu chifukwa ankaganiza kuti akumira.</i> Mwansanga anadzutsa Yesu ndi kumupempha kuti awapulumutse. Gwiritsani ntchito mawu amene iwo anayankhula. (<i>Mateyu 8:25</i>) Yesu anakhumudwa ndi ophunzira ake chifukwa analibe chikhulupiriro mwa lye. <i>Fotokozani kuti kukhala ndi chikhulupiriro ndi kudalira lye.</i> (<i>Mateyu 8:26a</i>)• Mphamvu za Yesu: Kenaka Yesu analetsa namondwe. (<i>Mateyu 8:26b</i>) Onani Marko 4:39.• <i>Tsindikani kuti namondweyo anasiya nthawi yomweyo kwathunthu!</i>• Kudabwa kwa ophunzira: (<i>Mateyu 8:27</i>) - <i>Fotokozani kuti pamene anaona mphamvu za Yesu pa mphepo ndi mafunde anazindikira kuti lye anali osiyana ndi iwo.</i>• <i>Onetsetsani kuti ana akumvetsa chifukwa chomwe Yesu anatha kuletsa namondwe. lye ndi Mwana wa Mulungu amene analenga chilichonse.</i>• <i>lye ali ndi ulamuliro pa chilichonse pa dziko lonse, kuphatikizapo nyengo. Limbikitsani ana kuti aganizire za nthawi imene iwo anadalira Yesu kuti ali ndi ulamuliro pa zonse zomwe zikuwachitikira.</i>• <i>Ife tikuyenera kukhulupirira kuti lye ndi Mwana wa Mulungu.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Yesu aletsa mphepo yamphamvu/Yesu aletsa namondwe.</p>
PHUNZIRANI	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – Mateyu 8:27.
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Kodi nkhanayi ikuchitikira kuti?• Kodi anayamba kulowa m'bwato ndi ndani?• Kodi madzi ankachita chiyani pamene namondwe anayamba?• Kodi Yesu ankachita chiyani pamene namondwe anayamba?• N'chifukwa chiyani ophunzira anamudzutsa Yesu?• N'chifukwa chiyani Yesu anakhumudwa chifukwa cha iwo?• Kodi Yesu analetsa zinthu ziwiri ziti?• Kodi Vesi Yoloweza ikupezeka pati?• N'chifukwa chiyani Yesu anatha kuletsa namondwe pomwe ophunzira ake sakanatha?• Kodi dzina la chinthu chimene Yesu anachita ndi liti? <p>Sewero: Zomwe tawerenga zikuonetsa kuti ophunzira khumi ndi awiriwo akhala m'bwato; ena achite phokoso la mphepo. M'tsogoleri wamkulu awerenge nkhanayi pamene ana akuchita zina zomwe zikufunana ndi mawu amene akuwerengawo.</p>

A3 Nkhani Yachinayi

Yesu apulumutsa Petulo – Iyi ndi nkhani ya Petulo kupempha thandizo.

	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Yesu apulumutsa Petulo poyankha pemphero lake lalifupi.• Ife tikuyenera kudalira Ambuye Yesu kuti tipulumutsidwe. <p>Ndime Yowerenga: <i>Mateyu 14:22-33</i> Vesi Yoloweza: <i>Mateyu 14:33</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Fotokozani kuti mukamakhala ndi munthu mumayamba kumudziwa bwino munthuyo. Thandizani ana kuti akumbukire zomwe Petulo waphunzira za Yesu.• Lolani ana apereke maganizo awo ndipo ngati muli ndi chipepala, mulembe pamenepo maganizowo. Chitsanzo: Yesu ndi Mwana wa Mulungu. Iye amachita zodabwitsa. Iye ali ndi ulamuliro pa nyanja.• Mu nkhani ya lero Petulo waphunzira zinanso zambiri za Yesu.
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Ophunzira analowa m'bwato ndi kunyamuka pamene Yesu anapita ku phiri kukapemphera. (Mateyu 14:22–23) - Fotokozani kufunika kwa pemphero m'moyo wa Yesu.• Namondwe: (Mateyu 14:24) - Kumbukirani za namondwe mu phunziro la sabata yatha ndipo fotokozani za namondwe uyunso. Yesu ankaona kuti ophunzira anali pa mavuto choncho lye anapita kwa iwo pakati pa usiku akuyenda pamwamba pa madzi. (Mateyu 14:25–27) Fotokozani zomwe ophunzira ankamva mu mtima mwawo ndi kuganiza. Onani mawu a Yesu achilimbikitso.• Pempho la Petulo: Petulo anafuna kutsimikiza ngati anali Yesu choncho anapempha kuti amulole kuti nayenso ayende pamwamba pa madzi! Yesu anati “Bwera” choncho Petulo anatuluka m'bwato ndi kuyamba kuyenda pamadzi kupita kumene kunali Yesu. (Mateyu 14:28–29) Zonse zinali bwino mpaka pamene Petulo anachotsa maso ake pa Yesu ndi kuyang'ana kukula kwa mafunde aja. Iye anayamba kumira!• Yesu apulumutsa Petulo: Gwiritsani ntchito mawu a Petulo kuti mufotokoze momwe anayitanira Yesu kuti amupulumutse. (Mateyu 14:30–32) Kenaka onse analowa m'bwato ndipo namondwe analeka. Fotokozani zomwe ophunzira anachita mu nkhani imeneyi. (Mateyu 14:33)• Petulo anafunika kupulumutsidwa kuti asamire. Ifenso tikufunika kupulumutsidwa ku machimo a m'miyoyo yathu. Ndi Ambuye Yesu wokha amene angatipulumutse. Yesu analangidwa chifukwa cha tchimo lathu pa mtanda. Ife tikuyenera kukhulupirira lye. <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Yesu apulumutsa Petulo.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – Mateyu 14:33.</p> <p><i>Fotokozani tanthauzo la kupembedza. Ophunzira anadabwa kwambiri ndipo anadzazidwa ndi chimwemwe chifukwa cha zomwe anaphunzira za Yesu. Fotokozani kuti kwina kulikonse, anthu amene amakonda Ambuye Yesu, awa ndi mawu opambana kwambiri amene angayankhule kuchokera m'mitima mwawo.</i></p>
KUMBUKIRANI	<p>Mafunso achokere mu nkhani za m'phunziro A3. Ngati muli ndi makadi mutha kujambula nsomba zosiyana makulidwe ake. Poyankha funso, ana asankhe kapena kugwira nsomba yomwe mwayika patsogolo panu. Nsomba iliyonse yalembedwa mapointi ake. Mukhale ndi magulu awiri ndipo muokhetse mapointi a gulu lililonse.</p> <ul style="list-style-type: none">• Kodi nkhani zonsezi zinachitikira kuti?• Tsirizani chiganizo ichi: “Bwerani nditsateni ndipo Ine...”• Kodi Yesu anayankhula mawu amenewa kwa yani?• Kodi Petulo anachita chiyani ataona kuti wagwira nsomba zambiri?• Tsirizani mawu awa, “Kodi munthu ameneyu ndi ndani...”• N'chifukwa chiyani Yesu anapita ku phiri?• Kodi ophunzira anachita mantha ndi chiyani?• Kodi Petulo anaphunzira chiyani kuchokera pa nkhani imeneyi?

A4 Nkhani Yoyamba

Petulo agona tulo – Iyi ndi nkhani ya nthawi imene Yesu ankapemphera kwa Atate ake.

	<p>Ife tikuphonzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none"> • Pemphero linali lofunika kwambiri pa moyo wa Ambuye Yesu. • N'kofunika kwa ife kuti tizipemphera. <p>Ndime Yowerenga: <i>Mateyu 26:36-46</i> Vesi Yoloweza: <i>Yohane 15:13</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none"> • Fotokozani zinthu zimene ndi zovuta kwa ana kuchita monga kuthamanga mtunda wautali, kukhala panso nthawi yayitali, ndi kukhala m'maso nthawi yayitali usiku. • M'nkhani ya lero, Yesu afuna mnzake Petulo amuthandize. Tiyeni tione ngati Petulo anachita zomwe Yesu ankafunazo!
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none"> • <i>Fotokozani komwe nkhani yayambira.</i> Yesu anadziwa kuti tsopano nthawi yayandikira yoti afe pa mtanda. Iye wadya kale mgonero komaliza ndi ophonzira. Nthawi zambiri Yesu anapemphera kwa Atate ndipo anadziwa kufunika kwa pemphero nthawi ngati imeneyi chifukwa cha zimene zikubwera. Iye anabwera ndi ophonzira ake m'munda kumene anakonda kupemphera. Usiku umenewu, akufuna abwenzi ake apadera atatu, Petulo, Yakobo ndi Yohane kuti akhale tcheru ndi kupemphera pafupi ndi Iye. • Yesu analangiza Petulo, Yakobo ndi Yohane kuti akhale tcheru ndi kumapemphera. (Mateyu 26:36–37) Kenaka Yesu anapita patsogolo pang'ono ndi kupemphera kwa Atate. <i>Fotokozani zomwe Yesu ankamva mu mtima mwake. Pemphero lake likuonetsa kuti anafuna kukondweretsa Atate pa chilichonse. (Mateyu 26:38–39)</i> Patatha ora limodzi, Yesu anapeza Petulo ndi anzake aja ali mtulo. <i>Fotokozani za kukhumudwa komwe Iye anali nako. (Mateyu 26:40–41)</i> • Yesu anakapemphera kachiwiri ndipo anadzapeza ophonzira ake ali mtulonso. (Mateyu 26:42–43) • Yesu anakapemphera kachitatu ndi kubweranso kudzapeza ophonzira aja ali mtulonso. <i>Kambiranani momwe Petulo andi anzake anakhumudwitsira Yesu. Iwo analepheranso kudzipempherera nthawi yovuta ngati imeneyi yomwe ankayenera kutero. (Mateyu 26:44–45)</i> • Nthawi imeneyi adani a Yesu anafika kudzamugwira. (Mateyu 26:45b–46) • <i>Potsiriza, tchulani kufunika kwa pemphero kwa ife kuti tilandire mphamvu kuchokera kwa Mulungu ndi kutithandiza kugonjetsa mayesero. Perekani zitsanzo zina zoyenera kuti zithandize ana kumvetsa.</i> • <i>Petulo ndi anzakewo analephera kumvera lamulo la Yesu la “kukhala tcheru ndi kupemphera” koma Yesu akufuna ife kuti tizimvera malamulo.</i> • <i>Mosiyana ndi ophonzira aja, Yesu sanatikhumudwitse. Iye anapemphera ndipo anapatsidwa mphamvu yopita pa mtanda kukapereka moyo wake chifukwa cha ife.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Petulo agona tulo/Petulo akugona.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – Yohane 15:13.</p>
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none"> • Kodi Yesu anapemphera kuti? • Kodi ndi ophonzira ati amene anafuna kuti azipemphera naye? • Kodi Yesu ankapempherera chiyani? • Kodi Yesu ankamva bwanji mu mtima mwake pamene ankapemphera? • Kodi Yesu anapemphera nthawi yayitali motani nthawi yoyamba? • N'chifukwa chiyani ophonzira analephera kupemphera? • Kodi Yesu anawapempha kangati kuti apemphere? • Kodi chinachitika ndi chiyani Yesu atamaliza kupemphera? • Kodi Vesi Yoloweza ikuchokera pati? • Kodi Yesu amatitcha ndani pamene tikumumvera?

A4 Nkhani Yachiwiri

Petulo adula khutu la munthu – Iyi ndi nkhani ya zomwe zinachitika pamene anthu ena ankagwira Yesu.

	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Yesu analolera kuti amugwire ndi kuphedwa m'malo mwathu.• Titha kuletsa mkwiyo pamene takumana ndi zovuta m'miyoyo yathu. <p>Ndime Yowerenga: <i>Mateyu 26:47-56</i> Vesi Yoloweza: <i>Aefeso 4:26</i></p>
MAWU OYAMBA	<p>Bwerezani nkhani ya m'mbuyomu yofotokoza zomwe zinachitika m'munda muja. Petulo ndi anzake sanapemphere monga mmene Yesu anawapempha kuti atero. Tsopano iwo akukumana ndi zinthu zovuta kwambiri. Kodi iwo achita chiyani tsopano?</p>
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Konzekekerani kuonetsa zomwe zinachitika nthawi imeneyi. Kunali kutada ndipo kunali bata...koma mwadzidzidzi kunamveka mdidi wa mapazi a asilikali. Kodi nthawi imeneyi Petulo ndi anzake aja anamva bwanji m'mitima mwawo?• Mwadzidzidzi, Yudas anatuluka pakati pa gulu la adani limeneli ndi kubwera kudzapsopsona Yesu. <i>Fotokozani kuti Yudas ndi ndani ndiponso kuti iyi inali njira yoti asilikali aja amuzindikire Yesu. Fotokozani tanthauzo la "kumupereka". (Onani Kalasi Yachiwiri Nthawiyabaibulo.) (Mateyu 26:47-50)</i>• Pamene Petulo anazindikira kuti anthuwa akugwira Yesu, iye anakwiya kwambiri ndipo anafuna kuteteza Yesu pomenya mmodzi mwa anthuwo. (Mateyu 26:51) - <i>Ndi chapafupi kwa ife kukwiya monga anachitira Petulo. Fotokozani chinthu chimodzi kapena ziwiri zomwe zimachitikira ana a msinkhu umenewu. Fotokozani kuti kunali kosafunika kuti Petulo ateteze Yesu chifukwa lye ankadziwa kuti zomwe zinkamuchitikira chinali chifuniro cha Mulungu. Yesu anali wokonzeka kulola adani ake kuti amugwire ndi kumupha. Iye anali wokonzeka kuchita zimenezi m'malo mwathu. Fotokozani kusiyana kwa pakati pa Yesu ndi Petulo. Petulo amene analephera kupemphera sanachite monga mmene Yesu akanafunira. (Mateyu 26:52-56)</i>• Ophunzira amene anali ndi mantha akulu anamusiya Yesu ndi kuthawa. <i>Kambiranani chifukwa chomwe anachitira zimenezi. (Mateyu 26:56b)</i> Ndi Petulo yekha amene anatsatira Yesu, koma chapatali kuopa kuti mwina naye angagwidwensho! <i>Thandizani ana kuti aone momwe Petulo anachitira zimenezi mosaonekera. (Mateyu 26:58)</i>• <i>Fotokozani kuti ngati ife ndi ake a Ambuye Yesu, tingathe kupemphera kwa lye kupempha kuti atithandize kuti tisakhale ndi mkwiyo koma tithe kudziretsa. Mzimu Woyera amene amakhala m'moyo wa Mkhristu amapereka mphamvu zokhalira moyo wabwino.</i>• <i>Yankhulani kuti pa nthawi imeneyo iwo akanapanda kukwiya kapena kuchita ndewu, zotsatira zikanakhala zosiyana.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Petulo adula khutu la munthu/Petulo achita ndewu.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – Aefeso 4:26. Fotokozani kuti ngati tili ndi mkwiyo tikuyenera kusiya kutero mofulumira!</p>
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Kodi ndi ndani amene anabwera m'munda pamodzi ndi adani a Yesu?• Kodi Yudas anachita chiyani pofuna kuwasonyeza Yesu?• Kodi Petulo anasolola chiyani pamene ankamugwira Yesu?• Kodi Petulo anadula chiwalo chiti cha thupi la munthu?• Kodi Yesu anawuza Petulo kuti achite chiyani?• Kodi Mkhristu angagonjetse bwanji mkwiyo?• Kodi ophunzira anachita chiyani pamene ankamugwira Yesu?• Kodi ndi ndani amene anatsatira Yesu chapatali? <p>Sewero: Atsogoreli achite sewero la gawo limodzi kapena awiri a nkhanayi pamene wina aonetsa mkwiyo wake monga zinachitikira mu nkhanayi.</p>

A4 Nkhani Yachitatu

Petulo anama za Yesu – Iyi ndi nkhani ya kufunika kwa kukhululukidwa.

	<p>Ife tikuphuzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Nthawi zina timakhala ndi mantha ndipo timakhumudwitsa abwenzi athu.• Pamene takhumudwitsa Ambuye Yesu, Iye ndi wokonzeka kutikhululukira. <p>Ndime Yowerenga: <i>Mateyu 26:69-75</i> Vesi Yoloweza: <i>Salimo 51:7</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Fotokozani za kuzindikira anthu kudzera m'mawu awo. Ngati ana akhala akugwiritsa ntchito foni angathe kuzindikira munthu amene akuyankhula naye popanda kuwuzidwa. Fotokozani kuti mawu amamveka mosiyanasiyana – mutha kupereka zitsanzo zingapo kuchokera m'dziko mwanu.• Lumikizani ndi nkhani ya sabata yatha – kumbutsani ana za kugwidwa kwa Yesu ndi za kuthawa kwa ophuzira ake. Koma Petulo anafuna kudziwa zomwe zimuchitikire Yesu.
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Petulo anatsatira mpaka m'bwalo la nyumba ya Mkulu wa Ansembe. (<i>Mateyu 26:69a</i>) - <i>Fotokozani kuti bwaloli linali kunjwa kwa nyumbayo. Ngati n'kotheke onetsani ana bwalo la pa nyumba ngati ilipo pafupi. Sewero – usiku wozizira, moto, alonda ndi antchito amene anali pamenepo.</i>• Mtsikana wantchito anazindikira Petulo ndipo anawuza ena kuti Petulo anali ndi Yesu. Petulo anakana ponena kuti sakudziwa zomwe mtsikanayo akuyankhula. (<i>Mateyu 26:69b-70</i>) - <i>Athandizeni ana kuzindikira kuti Petulo wayankhula zabodza.</i> Kunena zoonza iye anali ndi Yesu! Pezani zifukwa zomwe Petulo anayankhulira zabodza.• Petulo anasuntha pamenepo ndi kupita pa chipata cha nyumbayo, mtsikana winanso anamuzindikira. Petulo anakananso kuti sakumudziwa Yesu. (<i>Mateyu 26:71-72</i>) <i>Kwa ana amene akugwiritsa ntchito Kalasi Yachiwiri, fotokozani tanthauzo la mawu akuti "anakana".</i>• Patapita nthawi pang'ono, munthu winanso anati mawu a Petulo akufanana ndi mawu a otsatira Yesu. (Petulo anali wochokera ku Galileya monganso Yesu ndi omutsatira ena onse. <i>Lumikizani nkhani imeneyi ndi zomwe tayankhula kale m'mawu oyamba aja</i>). <i>Fotokozani za momwe Petulo anamvera mu mtima mwake pamene anakana Yesu kachitatu.</i>• Tambala analira ndipo Petulo anakumbukira zomwe Yesu anayankhula poyamba paja. (<i>Mateyu 26:34</i>) - <i>Fotokozani chifukwa chomwe Petulo anamvera chisoni kwambiri.</i> (<i>Mateyu 26:74b-75</i>)• <i>Petulo walakwa kwambiri. Iye sanalimbe mtima kuvomera kuti anali wotsatira wa Yesu m'malo mwake anayankhula zonama. Tonsefe timalakwitsa.</i>• <i>Ilipo nthawi imene ifenso timakhumudwitsa Ambuye Yesu kudzera mu zimene timayankhula ndi kuchita. Ambuye Yesu ndi wokonzeka kutikhululukira zolakwa zomwe tachita. Iye angathe kuchita zimenezi chifukwa anafa pa mtanda chifukwa cha machimo athu.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Petulo anama za Yesu/Petulo akana Yesu.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <i>Salimo 51:7.</i></p> <p><i>Fotokozani kuti ili ndi pemphero. Likutiwuzani kuti tikapempha Ambuye Yesu kuti atikhululukire machimo athu, zimakhala ngati akutisambitsa ndi kutiyeretisa – kuyera kuposa madzi owundana! Ngati n'kotheke fotokozani momwe madzi owundana mmene amaonekera.</i></p>
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Kodi Petulo ankadikira atakhala pati?• Kodi woyamba kuyankhula ndi Petulo anali ndani?• Kodi Petulo anayankhula kangati kuti sakumudziwa Yesu?• N'chifukwa chiyani Petulo anayankhula zabodza?• Kodi Petulo anamva tambala akulira kangati?• Kodi iye anakumbukira chiyani pamene anamva kulira kwa tambala?• N'chifukwa chiyani Petulo analira?• Kodi ife tichite chiyani pamene takhumudwitsa Ambuye Yesu?

A4 Nkhani Yachinayi

Petulo ayankhula ndi Yesu – Iyi ndi nkhanu ya Petulo kukonda Yesu.

	<p>Ife tikuphuzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Petulo anapatsidwa mpata wina woti aonetse chikondi chake pa Yesu atamukana.• Ambuye Yesu akufuna kuti tizimukonda. <p>Ndime Yowerenga: <i>Yohane 21:1-19</i> Vesi Yoloweza: <i>1 Yohane 4:19</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Funsani ana kuti akumbukire nkhanu zoyamba zimene anamva za Petulo. Kodi Petulo ankagwira ntchito yanji pamene Yesu ankamuyitana poyamba paja?• Fotokozani kuti kuyambira nthawi imeneyo pali zambiri zomwe zachitika. Petulo anali mmodzi mwa abwenzi apadera a Yesu, koma tsopano Petulo wakhumudwitsa Yesu (kumbukirani nkhanu zitatu zija).• Patapita nthawi pang'ono, Yesu anafa pa mtanda ndipo anauka kwa akufa. Pa nthawi ziwiri zosiyana, Yesu anakumana ndi ophuzira ake ndi kuwaonetsa kuti Iye ali moyo! Tsiku lina izi zitachitika, Petulo anaganiza zopitanso kukapha nsomba.
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Ophuzira anayesa kugwira nsomba usiku wonse koma sanagwire kanthu! (Yohane 21:3) - <i>Kambiranani momwe iwo ankamvera m'mitima mwawo – anali atatopa, a njala, okhumudwa.</i>• <i>Chithunzi cha zochitika - mmawa dzuwa litangotuluka, munthu wina wayima m'mbali mwa nyanja. Fotokozani zomwe anakambirana ophuzira ndi mlendo ameneyu. (Yohane 21:4-6a)</i>• Pamene anamvera malangizo a mlendo amenewu anagwira nsomba zambiri (153). Nthawi yomweyo Yohane anzindikira kuti munthuyo anali Yesu. Petulo anakondwa kwambiri ndipo analumphira m'madzi ndi kupita kukakumana naye. (Yohane 21:7-8)• Yesu anawakonza chakudya chammawa. (Yohane 21:9-14) - <i>Taganizirani momwe zinalili kudya chakudya chammawa m'mbali mwa nyanja ndipo fotokozani kuti ichi chinali chinthu chapadera ndi chosayembekezeka kuti Yesu anali pakati pawo.</i>• Atatha kudya, Yesu anayankhula ndi Petulo. Yesu anamufunsa Petulo katatu ngati amamukonda. (Yohane 21:15-19) - <i>Fotokozani kufunika kwa mafunso awa kwa Petulo. Ambuye Yesu anaonetsa kuti anamukhulukira Petulo ndipo anali ndi ntchito yapadera yoti amutume akachite. Kwa ana a Kalasi Yachiwiri, fotokozani momwe Petulo anaonetsera chikondi chake kwa Yesu katatu kameneka mosiyana ndi kumukana kwake kuja.</i>• <i>Limbikitsani ana za chikondi chawo pa Ambuye Yesu.</i>• <i>Kodi iwo angayankhe chiyani pa funso lomwe Yesu anafunsa Petulo? Yesu akufuna aliyense wa ife kuti tizimukonda ndi kumutumikira.</i>• <i>Mulungu amatikonda ndipo anaonetsa chikondi chake potumiza Mwana wake kudzatipulumutsa. Ife tikuyenera kuvomereza chikondichi poonetsa chikondi chatu pa Iye.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Petulo ayankhula ndi Yesu/ Petulo akonda Yesu.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – 1 Yohane 4:19.</p>
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Kodi Petulo ndi anzake anali m'madzi kuti agwire nsomba kwa nthawi yayitali yotani?• Kodi iwo anawuzidwa kuti aponye makoka awo mbali iti?• Kodi iwo anagwira nsomba zingati?• Kodi amene anayamba kuzindikira kuti anali Yesu ndi ndani?• Kodi ndi ndani amene anayamba kukafika komwe kunali Yesu?• Kodi Petulo anachita chiyani asanadziponye m'madzi?• Kodi anakonza chakudya chammawa ndi ndani?• Kodi iwo anadya chiyani mmawa umenewu?• Kodi ndi funso liti lomwe Yesu anafunsa Petulo katatu?• Kodi Vesi Yoloweza ikupezeka pati? <p>Sewero: Zina zomwe zikuyankhulidwa ana atha kuchita chionetsero (monga kupha nsomba, kuona munthu wachilendo m'mbali mwa nyanja, kulumphira m'madzi, kukoka nsomba zomwe agwira, kuwerenga nsomba); ndi kuonetsa pa nkhope zawo (monga kukhumudwa, kudabwa, kusangalala...). Ndi zothandiza kuwerenga zomwe zili m'Baibulo kwa ana ndi kuwapempha kuti aonetsero zimenezi.</p>

A5 Nkhani Yoyamba

Abrahamu achoka kwawo – Iyi ndi nkhani ya kukhulupirira Mulungu.

	<p>Ife tikuphuzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Abramam anamvera Mulungu pamene anachoka ku Uri ndi kupita ku dziko latsopano.• Ife tikuyenera kuonetsa kudalira kwathu mwa Mulungu pamene tikumumvera. <p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 12:1-9</i> Vesi Yoloweza: <i>Miyambo 3:5</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Fotokozani za kuchoka nyumba ina ndi kukalowa ina ngati anawo akudziwa zimenezi.• Kodi iwo angamve bwanji ngati akuchoka kwawo ndi kupita ku dziko lina? - kukondwera?• kudandaula? kumva chisoni? kusangalala? Perekani zifukwa.• Awuzeni za Abramam ndi kufotokoza momwe moyo wake unalili mu mzinda wa Uri – banja lake, abwenzi ake, nyumba yake, ziweto zake, chuma chake...Iye amakhala moyo wabwino kwambiri!
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Tsiku lina Mulungu anawuza Abramam kuti, “Tuluka m’dziko lako ndipo pita ku dziko limene ndidzakusonyeza.” (Genesis 12:1) - Kodi kunali kovuta kotani kwa Abramam Mulungu atamuwuzira kuti achoke kwawo (kusiya moyo wake wabwino kwawo osadziwa kumene akupita)?• Mulungu alonjeza Abramam. (Genesis 12:2-3) - Fotokozani kuti malonjezo a Mulungu anali ndi zinthu zonse zabwino, monga mtundu waukulu ndi dzina lotchuka. Iye anafuna kudalitsa Abramam. Mulungu akamadalitisa munthu, ndiye kuti Iye akuonetsa ubwino wake.• Abramam anamvera Mulungu. (Genesis 12:4) - Kodi mukuganiza kuti ndi chifukwa chiyani Abramam anamvera? (Iye anakhulupirira malonjezo/anadalira Mulungu.)• Fotokozani kuti Abramam anali ndi ndani – mkazi wake Sarai, m’dzukulu wake Loti, antchito ake ndiponso Mulungu anali nawo amene ankasonyeza njira. Fotokozani momwe iwo ankayendera pa ngamira ndi kumagona m’matenti pa ulendo wautali ngati umenewu wodzera m’chipululu.• Pomaliza Abramam anafika ku Kanaani. (Genesis 12:6-9)• Kodi nthawi imeneyi Abramam ankamva bwanji mu mtima mwake? Fotokozani kumanga guwa lansembe inali njira ya Abramam yosonyeza kuyamika Mulungu.• Kambiranani za nthawi zimene Mulungu amafuna kuti tizimudalira.• Fotokozani kuti izi zikutanthauza kuti tikudalira Mulungu kwathunthu; tikuyembekezera pa Iye kuti achita zonse mosadalira njira zathu kapena kuthekera kwathu. <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Abramam achoka kwawo/ Mulungu ayitana Abramam.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – Miyambo 3:5.</p> <p><i>Fotokozani kuti vesiyi ikunena zomwe Abramam anachita – iye anadalira Mulungu ndi mtima wake wonse m’ malo mochita zofuna zake.</i></p>
KUMBUKIRANI	<p>Lembani Inde/Ayi patsogolo pa ziganizo zili m’musimu pobwereza ndi kutsindika zomwe mwaphuzira. Khalani ndi nthawi ya mafunso!</p> <ul style="list-style-type: none">• Mulungu anayankhula kwa Abramam.• Abramam anachoka kwawo chifukwa kunali njala.• Mulungu analonjeza kudalitsa Abramam.• Abramam anali ndi zaka 70 pamene anachoka kwawo.• Abramam ankadziwa kumene ankapita.• Abramam anali ndi mwana wotchedwa Loti.• Mulungu anatsogolera Abramam kupita ku Kanaani.• Abramam ankakhala m’nyumba m’dziko latsopano.• Abramam ankasonyeza kudalira Mulungu pamene ankamumvera.• Mulungu akufuna kuti timudalire ndi kumumvera.

A5 Nkhani Yachiwiri

Abrahamu ndi Loti – Iyi ndi nkhani ya kudzikonda kwa Loti.

	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Loti anachita chisankho chosonyeza kudzikonda kwake ndipo zikuoneka kuti anachita chisankho cholakwika.• N'kofunika kwambiri kwa ife kuchita zisankho zoyenera. <p>Ndime Yowerenga: Genesis 13:1-18 Vesi Yoloweza: Genesis 13: 15</p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Kambiranani za zisankho zomwe ana amachita ndi kulola ena kuti akhale oyamba kusankha. Pezani chitsanzo chodziwika pakati panu.• Kambiranani za kukangana ndi momwe zimasokonezera ubale.
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Antchito a Abramu ndi a Loti ankakangana chifukwa cha dera lomwe iwo ankadyetserako ziweto zawo. (Genesis 13:5-7)• Abramu anadziwa kuti kukangana sichinthu chabwino, choncho anawuza Loti kuti asankhe kumene akufuna kupita ndi ziweto zake. (Genesis 13:8-9)• <i>Fotokozani momwe derali linalili, ndipo onetsani chisankho chomwe Loti anali nacho – chigwa cha Yorodani lomwe linali dziko lopanda mapiri ndiponso la madzi abwino kumene kunali msipu wambiri kusiyana ndi dera la ku mapiri komwe sikunali kwabwino. Kodi mukuganiza kuti Loti anasankha dera liti?</i>• Chisankho cha Loti. (Genesis 13:10-13) - <i>N'chifukwa chiyani Loti anachita chisankho chimenechi? (Iye anaona kuti dzikolo linali labwino ndipo ankafuna kuti likhale lake.) Loti anaonetsa khalidwe la dyera ndi lodzikonda. Fotokozani kuti chimene anasankha Loti sichinali chabwino monga mmene iye ankaganizira chifukwa anthu amene ankakhala kumeneko sankakondweretsa Mulungu.</i>• Abramu ndi Loti anasiyana koma Mulungu analonjeza Abramu kuti tsiku lina m'tsogolo, adzapereka kwa Abramu ndi zidzukululu zake dziko lonse ndiponso kumbali zonse. (Genesis 13:14-18)• <i>Kodi inu mukanakhala Abramu mukanamva bwanji mu mtima mwanu? Kodi mukanamva kuti wakuchenjeretsani? (Tsindikani kuti malonjezo a Mulungu kwa Abramu anali opambana kuposa dera lomwe Loti anasankha.)</i>• <i>Loti anachita chisankho cholakwika. Ife tikuyenera kuchita zisankho zolondola. Chisankho chopambana chomwe tingachite ndi kulola kuti Ambuye Yesu alowe m'miyoyo yathu ndi kutikhulukira machimo athu.</i>• <i>Tsindikani kuti Mulungu amadziwa zomwe ndi zabwino kwa ife ndipo Iye angathe kukwaniritsa zosowa zathu monga momwe anakwaniritsira zonse zimene Abramu ankazifuna. Fotokozani kuti titha kudalira Mulungu kuti adzasunga malonjezo ake.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Abrahamu ndi Loti/Abramu ndi Loti.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – Genesis 13: 15.</p> <p>Lumikizani nkhanayi ndi zomwe ana anamva.</p>
KUMBUKIRANI	<p>Nkhani ikuthera pamene Abramu akumanga guwa lansembe. Munthu akayankha funso molondola pa gulu aponye chinthu ichi kuti atenge mwala. (Genesis 13:1-6) Gwiritsani ntchito miyalala yeniyeni kapena yojambula pochita zimenezi. Gulu limene lipambane ndi limene likhale ndi miyala yambiri yomangira guwalo.</p> <ul style="list-style-type: none">• Kodi tikudziwa bwanji kuti Abramu anali ndi chuma chambiri?• Kodi ndi ndani amene ananena kuti mikangano ikuyenera kutha?• Kodi anayamba kusankha anali ndani?• Kodi Loti anaona mtsinje uti?• Kodi Loti anapita kuti?• Kodi chabwino kumene Loti anasankha chinali chiyani?• Kodi Mulungu anawuza Abramu ayang'ane kuti?• Kodi Mulungu analonjeza chiyani kwa Abramu? (dziko ndi zidzukululu)• Kodi Abramu anachita chiyani pa guwa limene anamanga lija?• Kodi chisankho chofunika kwambiri chomwe tingachite pa miyoyo yathu ndi chiti?

A5 Nkhani Yachitatu

Malonjezo a Mulungu kwa Abrahamu – Iyi ndi nkhani ya kukhulupirira malonjezo a Mulungu.

MAWU OYAMBA	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none"> • Popeza Mulungu amadziwa tsogolo, Iye amalonjeza zinthu zimene zidzachitike. • Mulungu akufuna kuti ife tikhulupirire malonjezo ake. <p>Ndime Yowerenga: Genesis 15:1-7 Vesi Yoloweza: Genesis 15:6</p>
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none"> • Perekani chitsanzo cha lonjezo lomwe ana angachite. Tsindikani za kukhulupirira kumene akuyenera kuonetsa pamene akudikirira ndiponso chisangalalo chawo pamene akudikirira kukwaniritsidwa kwa lonjezolo. (Mutha kufotokoza za lonjezo lomwe pa zifukwa zina silingakwaniritsidwe.) • Ife monga anthu timalephera kusunga malonjezo athu, koma Mulungu nthawi zonse amasunga malonjezo ake! <ul style="list-style-type: none"> • Mulungu anayankhula ndi Abramam kudzera m'maloto ndipo analonjezo kuti adzakhala ndi mwana wamwamuna. (Genesis 15:1, 4) - Lumikizani izi ndi malonjezo ena oyamba aja kwa Abramam. Tafotokozani momveka bwino kuti nkhani iyi inali yosangalatsa kwambiri kwa Abramam amene nthawi imeneyi anali ndi zaka zoposera 90. • Mulungu anaonetsa Abramam nyenyezi ndi kumuuzza kuti zidzukuluka zake zidzachulukira ngati nyenyezizo! (Genesis 15:5) - Taganizirani za chintchito choyesera kuwerenga nyenyezi! Ana nawonso afotokoze za kudabwitsa kwa nyenyezi ndi kwa Mlenji wake. • Abramam anakhulupirira lonjezo la Mulungu. (Genesis 15:6) Pezani zifukwa zomwe zinachititsa Abramam kuti akhulupirire Mulungu. • Mulungu anapereka mayina atsopano kwa Abramam ndi Sarai. (Genesis 17:5, 15) - Dzina latsopano la Abramam likutanthauza “kholo la anthu ambiri” kuti iye nthawi zonse azikumbukira malonjezo a Mulungu. • Mulungu watlonjeza ife m'Mawu ake, Baibulo. Perekani zitsanzo zina za malonjezo a Mulungu kwa ife pamene tamukhulupirira. • Mulungu amakondwera pamene tikhulupirira zomwe Iye akunena. <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Malonjezo a Mulungu kwa Abrahamu/Malonjezo a Mulungu.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – Genesis 15: 6</p>
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none"> • Kodi Mulungu analonjeza kale Abramam kuti adzakhala wotsogolera chiyani? • Kodi Mulungu analonjeza Abramam chiyani kudzera m'maloto kapena m'masomphenya? • Kodi mkazi wa Abramam anali ndani? • Kodi Mulungu anamuonetsa Abramam chiyani? • Kodi Mulungu anafananiza nyenyezi ndi chiyani? • Kodi Abramam anachita chiyani Mulungu atamalonjeza izi? • Kodi dzina latsopano la Abramam ndi liti? • Kodi dzina latsopano la Sarai ndi liti? • Kodi Mulungu akufuna kuti tichite chiyani tikadziwa malonjezo ake kwa ife? • Kodi mawu akuti “kukhulupirira” amatanthauza chiyani?

A5 Nkhani Yachinayi

Abrahamu ndi alendo – Iyi ndi nkhani ya kukwaniritsidwa kwa malonjezo a Mulungu.

	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">Mulungu ankatumiza mauthenga ake m'njira zosiyanasiyana, makamaka nthawi imene Baibulo linali lisanalembedwe. Amithenga atatu ofunika kwambiri anabwera ndi uthenga kwa Abrahamu wochokera kwa Mulungu.Mulungu ndi wokhulupirika pa malonjezo ake - palibe chimene chikhoza kumukanika Yehova. <p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 18:1-15</i> Vesi Yoloweza: <i>Genesis 18:14</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">Fotokozani zomwe zimachitika kwanuko kukabwera alendo amene simumawayembekezera. Gwiritsani ntchito zinthu kuti muonetse zimenezi kapena mupeze ana ena omwe akhale ngati alendo pakati.Konzekerani kufika kwa alendo a Abrahamu – Abrahamu ankapuma pa khomo la tenti yake nthawi ya masana ... pamene anaona anthu ena kuyandikira kumene analipo. Kodi amenewa anali ndani?
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">Abrahamu analandira alendo aja ndipo anawapatsa madzi akumwa ndi chakudya. (Genesis 18:2-8) - <i>Fotokozani zomwe anachita Sara. Muyankhule kuti anawo akhale ndi chithunzi m'maganizo awo cha nkhani imeneyi – dzuwa likuwala, kusambitsa mapazi awo ndi madzi ozizira, kununkhira kwa chakudya...</i>Atatha kudya, alendo atatu aja anapereka uthenga kwa Abrahami woti Sara adzakhala ndi mwana wamwamuna chaka chotsatiracho. (Genesis 18:9-10) - <i>Kodi alendowo anadziwa bwanji zimenezi? Fotokozani kuti alendo amenewa anali ndani – Amithenga a Mulungu ochokera kumwamba – mmodzi mwa iwo anali Ambuye Yesu ndipo enawo anali angelo. Kambiranani za momwe Abrahamu anamvera mu mtima mwake atamva uthengawu. Malonjezo a Mulungu anali pafupi kukwaniritsidwa!</i>Sara anaseka chifukwa ankaganiza kuti sizingatheke koma Ambuye analonjeza kuchita zosathekazo! (Genesis 18:11-15) - <i>Kambiranani za momwe Mulungu anamvera mu mtima mwake pamene Sara anaseka.</i>Chaka chitatha, Sara anabereka mwana wamwamuna. (Genesis 21:1-7) - <i>Tayeserani kuganizira chimwemwe chimene iwo anali nacho. Kodi Mulungu anasunga lonjezo lake? Kwa ana a Kalasi Yachiwiri, fotokozani tanthauzo la dzina la Isake (kuseka).</i>Titha kudalira Mulungu kuti adzasunga malonjezo ake onse kwa ife. Palibe chomukanika lye – lye ali chomwecho mpaka lero! Uyutu ndi Mulungu wodabwitsa amene tiyenera kumudalira! <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Abrahamu ndi alendo.</p>
PHUNZIRANI	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza - Genesis 18:14.
KUMBUKIRANI	<p>Mafunso awa akuchokera mu nkhanayi. Gwiritsani ntchito mafunso amenewa kapena pezani mafunso kuchokera m'nkhani zonse za A5.</p> <ul style="list-style-type: none">Kodi alendowa anafika nthawi yanji?Kodi Abrahamu anali kuti nthawi imeneyi?Kodi Abrahamu anawuza Sara kuti achite chiyani?Kodi iwo anadyanso chiyani?Kodi Sara anali kuti pamene amithengawa ankafotokoza nkhanayi?N'chifukwa chiyani Sara anaseka?Kodi panapita nthawi yayitali yotani mpaka pamene Sara anakhala ndi mwana?Kodi mwanayo anamutcha ndani?Kodi Abrahamu anali ndi zaka zingati pamene Isake ankabadwa?Ganizirani zifukwa ziwiri zomwe zinachititsa Abrahamu ndi Sara kukhala osangalala. (Iwo anakhala ndi mwana, Mulungu anasunga lonjezo lake kwa iwo) <p>Sewero: Ana atha kusangala ndi gawo loyamba la nkhani iyi ngati angachite sewero. Konzani zomwe anawo akuyenera kuchita. Munthu wamkulu atenge gawo la Abrahamu, Sara, antchito, alendo atatu. Komanso mutha kukhala m'magulu aang'ono, ana atha kumayerekeza kapena kuyankhula.</p>

A6 Nkhani Yoyamba

Abrahamu amvera Mulungu – Iyi ndi nkhani ya kukonda Mulungu kuposa zonse.

	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Abrahamu anakonda Mulungu kuposa wina aliyense kapena china chilichonse.• Ifenso tikonde Mulungu ndi mitima yathu yonse. <p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 22:1-9</i> Vesi Yoloweza: <i>Genesis 22: 8</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Funsani ana kuti akuwuzazi zinthu zina zomwe ndi zofunika kwambiri kwa iwo – Kodi chinthu chofunika kwambiri pa moyo wanu ndi chiyani? N'chifukwa chiyani chili chofunika?• Kenaka afunse kuti angamve bwanji mu mtima ngati wina atawawuza kuti apereke zinthu zimenezo – Kodi mungakonde kuzipereka? Nanga mungamve bwanji ngati wina atenga zimenezo? Fotokozani kuti nkhani ya lero Abrahamu akupereka chinthu chimene chinali chofunika kwambiri kwa iye.
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Mulungu anasunga lonjezo lake kwa Abrahamu ndi Sara ndipo anawapatsa mwana wamwamuna. Dzina lake Isake. Iwo ankamukonda kwambiri. (<i>Genesis 21:1-3</i>)• Tsiku lina Mulungu anawuza Abrahamu kuti atenge Isake ndi kupita naye ku phiri la Moriya. Nthawi imene Isake anali kanyamata. Mulungu ankafuna kuti Abrahamu apereke nsembe mwana wake Isake kwa Iye. Mulungu ankamuyesa Abrahami kuti aone ngati amamukondadi Iye. Ngakhale izi zinamvetsa chisoni Abrahamu, iye anakhulupirira Mulungu ndipo anachita zomwe anamuwuza kuti achite.• (<i>Genesis 22:1-2</i>) - <i>Abrahamu anakonda Mulungu ndi mtima wake wonse. Tsopano anamvera Mulungu ndipo anali wokonzeka kumumvera ngakhale pamene Mulungu ankamuwuza kuti achite chinthu chovuta ngati chimenechi.</i>• Mmawa kwambiri, Abrahamu anatenga zonse za pa ulendowu. Iye anadula nkuni zootchera nsembe, anatenga antchito awiri ndi bulu wake. (<i>Genesis 22:3</i>)• Patapita masiku atatu, anafika ku phiri limene Mulungu analisankha. Abrahamu anawuza antchito ake kuti akhale pamalo ena ndi kumudikira pamodzi ndi bulu. Isake ananyamula nkuni pomwe abambo ake ananyamula mpeni ndi moto. (<i>Genesis 22:4-6</i>)• Iwo anayamba kukwera phiri, Isake anafunsa abambo ake kuti mwanawankhosa woti akapereke nsembe ali kuti? Abrahamu anayankha kuti “Mwana wanga, Mulungu adzapereka mwanawankhosa.” (<i>Genesis 22:7-8</i>)• <i>Abrahamu anamvera Mulungu chifukwa ankamukonda Iye. Mulungu akufuna kuti ife tizimukonda ndi mitima yathu yonse ndiponso kumumvera zomwe zimene akutiwuzazi kuti tichite.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Abrahamu amvera Mulungu.</p>
PHUNZIRANI	Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – <i>Genesis 22: 8</i> .
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Kodi mwana wa Abrahamu dzina lake anali ndani?• Kodi dzina la phiri lomwe Mulungu anawuza Abrahamu kuti apite linali?• Kodi Abrahamu anatenga antchito angati?• Kodi Abrahamu anatenga nyama yanji?• Kodi anayenda masiku angati kuti akafike ku phiri limeneli?• Kodi Abrahamu anati ndi yani amene “adzapereka mwanawankhosa”?• Kodi Abrahamu anakonda ndani kuposa wina aliyense kapena china chilichonse?• Kodi ife tikuyenera kukonda ndani ndi mitima yathu yonse?

A6 Nkhani Yachiwiri – KALASI 0 ndi Yoyamba
Chisamaliro cha Mulungu – Iyi ndi nkhani ya momwe Mulungu anasamalira Hagara.

	<p>Ife tikuphuzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none"> • Mulungu anapereka zosowa za Hagara ndi Ismaeli. • Mulungu angathe kukwaniritsa zosowa zathu. <p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 21:8-20</i> Vesi Yoloweza: <i>1 Petulo 5:7</i></p>
<p align="center">MAWU OYAMBA</p>	<ul style="list-style-type: none"> • Fotokozani za kufunika kwa madzi. Kambiranani za kukhala ndi ludzu ndi zotsatira zake ngati osamwa madzi pamene tili ndi ludzu. • Lumikizani nkhanayi ndi zochitika pakati panu; thandizani ana kuti azindikire kufunika kwa madzi abwino ndi kuti ndi ofunika kwambiri. • Kambiranani za malo osiyanasiyana kumene kumachokera madzi: madamu, mitsinje, m'mapiri, m'zitsime, pa mpope, m'botolo. Ngati n'kotheke onetsani zithunzi kapena zosungira madzi zosiyanasiyana
<p align="center">PHUNZITSANI</p>	<ul style="list-style-type: none"> • Fotokozani kuti Hagara ali mmodzi mwa antchito a Abrahamu ndi Sara. Iye anali ndi mwana wotchedwa Ismaeli. Tsiku lina Sara anakwiya chifukwa cha Hagara ndi mwana wake, ndipo anaganiza kuti asakhalenso pamodzi ndi Hagara ndi mwana wakeyo. Abrahamu sanafune kuwachotsa koma Mulungu anamufotokozera kuti kunali koyenera kuti achoke. (Genesis 21:8–13) • Tsiku lotsatira, Abrahamu anapereka zakudya ndi madzi kwa Hagara ndi Ismaeli kuti apite nazo. Fotokozani kuti nthawi imeneyi kunalibe madzi a m'botolo, koma ankagwiritsa ntchito zikopa za nyama ngati mabotolo awo. Hagara anasenza chakudya ndi madzi ndi kuyamba ulendo wawo kulowera ku chipululu. Fotokozani momwe nyengo inalili - kunali kotentha kwambiri ndi kowuma, kunali mitengo yochepa kwambiri kapena udzu ndipo kunalibe magolosale! Funsani ana za “kumalo otentha” kumene iwo anakhalako. Siyanitsani zomwe zinachitika kwa iwo ndi zomwe zinachitikira Hagara ndi Ismaeli. Kodi iwo ankamva chiyani mu mtima mwawo (chisoni, kutopa chifukwa choyenda nthawi yotentha, kupweteka kwa mapazi ndi ludzu). Fotokozani za kuyimayima kwawo kuti amwe madzi ndi kuti madzi awo anayamba kuchepa. Funsani ana zomwe zinachitika madzi atatha. (Genesis 21:14) • Hagara ankamvera chisoni kwambiri mwana wake Ismaeli. Iye ankadziwa kuti mwana wake adwala chifukwa cha kutentha kwa dzuwa choncho anamugoneka pa mthunzi. Hagara anakhala panso pafupi ndi kuyamba kulira. Zinkaoneka kuti anali okha awiri popanda wina woti n'kuwathandiza. Kumbutsani ana kuti alipo wina amene amadziwa zinthu zonse. Kodi ameneyo ndi ndani? (Genesis 21:15-16) • Tsimikizirani kuti Mulungu ankadziwa kumene kunali Hagara ndi Ismaeli ndiponso za mavuto awo onse. Mulungu anamva kulira kwa Ismaeli. Werengani mawu amene anayankhula kwa Hagara. (Genesis 21:17-18) Fotokozani kuti Mulungu ankadziwa dzina la Hagara, monga momwe iye amadziwira mayina athunso. Zochitika zonse zinali m'manja mwa Mulungu. Ismaeli sakanafa chifukwa cha kutentha kwambiri kwa dzuwa. Mulungu anali ndi dongosolo la moyo wa Ismaeli. • Nthawi imeneyi Mulungu anaonetsa Hagara chitsime cha madzi. Thandizani ana kuti amvetse za kudabwitsa kwa chisamaliro cha Mulungu – ichi ndiye ankachifuna nthawi imeneyi, pamalo amene ankachifuna ndiponso nthawi imene ankachifuna! Ganizirani za momwe Hagara ankamvera mu mtima mwake pamene ankatunga madziwo kudzazitsa botolo lake la chikopa ndiponso momwe ankamvera Ismaeli mu mtima mwake pamene ankamwa madzi ozizira abwinowa. (Genesis 21:19) • Nkhani ikuthera pamene akufotokoza kuti Mulungu anali ndi mwanayo pamene anakakula. Baibulo limaphunzitsa kuti ndi chinthu chabwino kwambiri kukhala ndi Mulungu pamene tikanali aang'ono komanso pa moyo wathu wonse. <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Chisamaliro cha Mulungu.</p>
<p align="center">PHUNZIRANI</p>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – 1 Petulo 5:7.</p> <p>Fotokozani kuti nthawi iliyonse imene tili ndi mantha titha kutsimikizika kuti Mulungu akudziwa. Iye amafuna kuti timupatse nkhaba zathu zonse. Iye amasalama za ife kuposa momwe tingaganizire.</p>
<p align="center">KUMBUKIRANI</p>	<p>Mutha kuyankhula zambiri za chisamaliro cha Mulungu ndi kufunsa ana kuti afotokoze njira zimene iye amaonetsera potisamalira. Mutha kugwiritsa ntchito zithunzi za mawu akuluakulu akuti “Iye amatisamalira”. Kapena muthanso kuyankhula nkhani yomweyi ya madzi. Mwana aliyense ajambule botolo la madzi, lembanipo ndipo mudule ndi kumata pamene pali mawu a Vesi Yoloweza kapena mawu akuti “Zikomo Mulungu chifukwa cha madzi abwino akumwa tsiku lililonse.”</p>

A6 Nkhani Yachiwiri – Kalasi Yachiwiri
Abrahamu amvera Mulungu

	<p>Ife tikuphonzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none"> • Mulungu anapereka nkhusa yayimuna m'malo mwa Isake. • Yesu analowa m'malo mwathu pa mtanda chifukwa cha machimo athu. <p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 22:9-14</i> Vesi Yoloweza: <i>Agalatiya 2:20</i></p>
<p align="center">MAWU OYAMBA</p>	<ul style="list-style-type: none"> • Funsani ana kuti aganizire kuti ali pafupi kulandira chilango chifukwa cha zomwe achita. – Kodi iwo angamve bwanji mu mtima mwawo? • Kenaka funsani ana kuti aganizire kuti munthu wina walandira chilangocho m'malo mwawo. – Kodi iwo angamve bwanji mu mtima mwawo? • Fotokozerani ana kuti nkhusa ya lero ndi ya chinthu china chomwe chikuchitika m'malo mwa Isake.
<p align="center">PHUNZITSANI</p>	<p>Kumbutsani ana pomwe nkhusa yafika.</p> <ul style="list-style-type: none"> • Potsiriza pa ulendo, Abrahamu ndi Isake afika pamwamba pa phiri, pamene amanga guwa lansembe la miyala. Isake wagona pa guwapo. (Genesis 22:9-10) • Abrahamu tsopano akufuna kupereka nsembe Isake kwa Mulungu, mngelo akuyankhula kuchokera kumwamba ndipo akuwuzza Abrahamu kuti asaphe mnyamatayo. Abrahamu waonetsa kuti amakonda Mulungu kwambiri. (Genesis 22:11-12) • Kenaka Abrahamu anatukula maso ake ndipo anaona nkhusa yayimuna itakodwa mu ziyangoyango. Iye anagoneka nkhusayo pa guwa lansembe m'malo mwa Isake. (Genesis 22:13) • <i>Kodi inu mukuganiza kuti Abrahamu ndi Isake anamva bwanji m'mitima mwawo pamene anazindikira kuti nkhusayo ilowa m'malo mwa Isake?</i> • <i>Pamene Yesu anafa pa mtanda, anafa m'malo mwathu. Tonse tachita zinthu zolakwa, koma Yesu analangidwa chifukwa cha kulakwa kwathu pamene anafa.</i> • <i>Yesu anatifera chifukwa amatikonda ndipo sanafune kuti ife tilangidwe chifukwa cha machimo athu. Iye akufuna kuti tizimukonda Iye ndi kumuyamika chifukwa chotenga malo athu.</i> • <i>Kodi inu mukumva bwanji mu mtima mwanu pamene mwazindikira kuti Yesu amakukondani kwambiri mpaka kufa m'malo mwanu?</i> • <i>Kodi tingaonetsa bwanji kuti timamukonda Yesu?</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Abrahamu amvera Mulungu</p>
<p align="center">PHUNZIRANI</p>	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – Agalatiya 2:20.</p>
<p align="center">KUMBUKIRANI</p>	<ul style="list-style-type: none"> • Kodi Abrahamu anamanga kuti guwa lansembe? • Kodi anagwiritsa ntchito chiyani pomanga guwalo? • Kodi ndi ndani anayankhula kuchokera Kumwamba? • Kodi mngelo anamuwuzza Abrahamu chiyani? • Kodi Abrahamu anaonetsa chiyani kwa Mulungu? • Kodi ndi chiyani chinalowa m'malo mwa Isake pa guwapo? • Kodi ndi ndani anatenga malo athu pa mtanda? • N'chifukwa chiyani Yesu anafa pa mtanda?

A6 Nkhani Yachitatu

Thandizo la Mulungu – Iyi ndi nkhani ya Mulungu kuonetsa njira.

	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Wantchito anapempha Mulungu kuti amuthandize ndipo Mulungu anamuthandiza.• Mulungu adzatithandizanso ngati tingamupemphe. <p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 24:1-28</i> Vesi Yoloweza: <i>Genesis 24: 27</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Funsani ana aganize za anthu amene amawathandiza – Kodi amakuthandizani ndi ndani? Kodi amakuthandizani ndi zinthu zotani? Kodi inu mumamva bwanji mu mtima pamene akukuthandizani?• Perekani mpata kwa ana kuti afotokoze nthawi zimene iwo anathandiza munthu wina.• Fotokozerani ana kuti nkhani ya lero ndi ya Mulungu kuthandiza munthu wina.
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Abrahamu anali atakalamba kwambiri, koma asanamwalire iye ankafuna kuonetsetsa kuti Isake akhale ndi banja labwino. Choncho analamula m'tsogoleri wa antchito ake kuti akamupezere mkazi mwana wakeyo. Abrahamu anamuwuzwa kuti adalire Mulungu kuti adzamutsogolera kwa mkazi woyenera. (Genesis 24:1-9) - <i>Kodi mukuganiza kuti wantchitoyo anamva bwanji mu mtima mwake pamene Abrahamu anamuwuzwa kuti akapezere Isake mkazi?</i>• Wantchitoyo anatenga ngamira khumi za Abrahamu ndi kuyamba ulendo umenewu. Iye atayenda masiku ambiri, anayima pa chitsime cha madzi kufupi ndi mzinda wa Nahori. Inali nthawi ya kumadzulo pamene atsikana amabwera kudzatunga madzi pa chitsimepo. (Genesis 24:10-11)• Wantchitoyo anapemphera kwa Mulungu kuti amuonetse mmodzi mwa atsikanawo amene adzakhale mkazi wa Isake. Iye ananena kuti adzapempha madzi akumwa ndipo ngati mtsikanayo adzaperekanso madzi kwa ngamira zake, pamene iye adzadzwiwa kuti ameneyo ndi mkazi amene Mulungu wasankha kuti akhale mkazi wa Isake. (Genesis 24:12-14)• Pasanapite nthawi, iye anaona mtsikana wokongola akubwera ku chitsimeko. Dzina lake linali Rebeka. Pamene anapempha madzi akumwa, iye mosangalala anamupatsa ndipo anapereka kwa ngamira zake. Kodi wantchitoyo anaganiza chiyani? <i>Kodi anamva bwanji mu mtima mwake?</i> (Genesis 24:15-21)• Iye atapereka mpatso kwa mtsikanayo zochokera kwa Abrahamu, anamufunsa ngati kwawo kunali malo kuti iye akagone usiku umenewo. Pamene anamuwuzwa kuti anali ndi malo ambiri, wantchitoyo anaweramitsa mutu wake ndi kuyamika Mulungu chifukwa choyankha mapemphero ake ndi kumuthandiza kupeza mkazi woyenera. (Genesis 24:22-27)• <i>Kodi inu anayamba akupatsanipo ntchito yovuta kuti mugwire? Perekani zitsanzo zoyenera.</i>• <i>Kodi wantchitoyu anapempha thandizo kwa ndani?</i>• <i>Kodi ife tingapemphe ndani kuti atithandize? Mulungu akufuna kutithandiza ndi kutitsogolera pamene tikuchita zisankho ndi kukhazikitsa fundo. Iye adzatithandiza kusankha moyenera.</i> <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Thandizo la Mulungu.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – Genesis 24: 27.</p>
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Kodi ndi ndani anapita kukafuna mkazi wa Isake?• Kodi wantchitoyo anatenga ngamira zingati pa ulendowu?• Kodi wantchitoyo anayima pati?• Kodi inali nthawi yanji?• Kodi wantchitoyu anapempha ndani kuti amuthandize kupeza mkazi woyenera?• Kodi mtsikana anabwera pa chitsimepo dzina lake anali ndani?• Kodi iye anachita chiyani pothandiza wantchitoyo?• Kodi wantchitoyo anachita chiyani pamene anazindikira kuti Mulungu wamuthandiza? <p>Ngati muli ndi nthawi, ana ajambule chithunzi chawo akuthandiza munthu wina.</p>

A6 Nkhani Yachinayi

Chisankho cha Mulungu – Iyi ndi nkhani ya Isake kukwatira Rebeka.

	<p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ul style="list-style-type: none">• Rebeka ndi Isake anatsatira chikonzero cha Mulungu ndipo anali osangalala kwambiri.• Pamene tidalira Mulungu ndi kutsatira njira yake tidzakhala osangalala. <p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 24:28-67</i> Vesi Yoloweza: <i>Salimo 144:15</i></p>
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none">• Funsani ana ngati anapitapo ku ukwati – Kodi ukwatiwo unali wa ndani? Kodi anavala chiyani? Kodi pa ukwatiwo panachitika chiyani? Kodi mkwati ndi mkwatibwi anali osangalala?• Uzani ana kuti nkhani ya lero ndi ya mmene ukwati unkachitikira m’Baibulo.• Nkhani iyi ndi yosiyana ndi mmene ukwati umachitikira m’dziko lanu.
PHUNZITSANI	<ul style="list-style-type: none">• Kumbutsani ana pamene nkhani yafika.• Rebeka anafulumira kupita ku nyumba kwawo kukawuza abale ake zomwe zinachitikazo. Mlongo wake Labani anathamanga kupita ku chitsime kukatenga wantchitoyo ndi kubwera naye ku nyumba kwawo ndi kumulonjera. Koma wantchito asanadye chakudya chamadzulo, anafotokozera abale a Rebeka cholinga cha kubwera kwake. (Genesis 24:28-49)• Bambo a Rebeka pamodzi ndi Labani anavomereza kuti anali Mulungu amene anatsogolera wantchitoyo kwa Rebeka. Mosataya nthawi anamulola wantchitoyo kuti atenge Rebeka ndi kupita naye kuti akakhale mkazi wa Isake. Wantchitoyo anayamika Mulungu chifukwa choyankha pemphero lake. Kenaka anapereka mphatso zambiri kwa Rebeka ndi abale ake. (Genesis 24:50-53)• M’mawa, iwo anafunsa Rebeka ngati anali wokonzeka kupita ndi wantchitoyo kuti akakhale mkazi wa Isake. Rebeka anavomereza kupita naye. (Genesis 24:54-61) - <i>Kodi Rebeka ankamva bwanji mu mtima mwake? (Mantha pang’ono chifukwa sankamudziwa Isake ndi abale ake, koma anali ndi chisangalala chifukwa ichi chinali chikonzero cha Mulungu pa moyo wake!)</i>• Komwe kunali Abrahamu, Isake ankadikira ndi kumalingalira zomwe zinamuchitikira wantchitoyo. Tsiku lina chakumadzulo akuyenda m’munda, anaona ngamira zikubwera. Mosachedwa analandira Rebeka ku nyumba yake yatsopano mu tenti ya amayi ake. Isake anamukonda Rebeka kwambiri ndipo anakhala mkazi wake. (Genesis 24:61-67)• <i>Kodi inu mukuganiza kuti Isake anamva bwanji mu mtima mwake pamene anaona mkazi wakeyo? (Mwina anasangalala kwambiri komanso mwina ankachita mantha pang’ono chifukwa anali asanakumane naye Rebeka, koma iye anadalira chikonzero cha Mulungu ndipo anali wosangalala kutenga Rebeka kukhala mkazi wake.)</i>• Isake ndi Rebeka onse awiri anali osangalala kwambiri chifukwa anadalira Mulungu ndi kutsatira chikonzero chake. Mulungu amafuna kuti tizimudalira ndi kutsatira chikonzero chake. Ife tikachita zimenezi, tidzakhala ndi chimwemwe ndi chisangalala chachikulu. <p>Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Chisankho cha Mulungu.</p>
PHUNZIRANI	<p>Phunzitsani ndi kufotokoza kufunika kwa Vesi Yoloweza – Salimo 144:15.</p> <p>Vesi iyi ikufotokoza za kusangalala komwe tingakhale nako ngati tikutsatira chikonzero cha Mulungu pa miyoyo yathu.</p>
KUMBUKIRANI	<ul style="list-style-type: none">• Kodi mlongo wa Rebeka dzina lake ndani?• Kodi wantchitoyo anachita chiyani asanadye chakudya chamadzulo?• N’chifukwa chiyani abale a Rebeka anavomera kuti apite kukakhala mkazi wa Isake?• Kodi wantchitoyo anapereka chiyani kwa Rebeka ndi kwa abale ake?• Kodi iwo anati ndi ndani amene anatsogolera wantchitoyo kwa Rebeka?• Kodi Rebeka ananyamuka liti pamodzi ndi wantchitoyo?• Kodi ndi ndani amene ankayenda m’munda pamene wantchitoyo ankabwera ndi Rebeka?• N’chifukwa chiyani Isake ndi Rebeka anali osangalala m’banja mwawo?• Kodi ndani angatisangalatse kuposa wina aliyense kapena chilichonse?

Malangizo a Aphunzitsi a Kachongedwe ka Maphunziro

Maphunziro a Kalasi Yoyamba

- Sabata lililonse pali mapeji anayi amene akufunika kuchekenira ndi kulembamo mawu pang'ono.
- Sabata lililonse pali marikisi 20 amene akuyenera kuperekedwa kuchokera pa marikisi 80 a mwezi onse.
- Ana amene akuphunzira maphunziro a Kalasi Yoyamba iwo sakuyenera kuwerenga chifukwa sangathe kuwerenga bwino ndipo tikuyembekezera makolo/owang'anira/atsogoleri awo kuwathandiza.

Maphunziro a Kalasi Yachiwiri

- M'buku muli maphunziro anayi pa sabata.
- M'phunziro lililonse muli nkhani. Ophunzira akuyenera kupeza mawu osiyanasiyana m'phunziro, ndi kuchekenira, kutsiriza Mavesi Oloweza ndi zina zambiri.
- Sabata lililonse pali marikisi 20 pa marikisi 80 a mwezi uliwonse pamene atsiriza maphunziro onse molondola.

FUNDO ZA KACHONGEDWE

GUTANGA AMANOTA

Choyamba aphunzitsi akupemphedwa kuti:

- Onani phunziro lililonse ndipo chongani moyenera zolondola kapena zolakwitsa.
- Perekani marikisi amene mwalangizidwa kutero.
- Nthawi zonse chongani pogwiritsa ntchito mitundu yosiyana ya zolemba, CHONGANI yankho lolondola.
- Lembani yankho lolondola poyenera kutero ndi kukonza mawu olakwika kalembedwe ake, koma MUSACHOTSE marikisi.
- Perekani marikisi ochepa pa yankho lolondola mbali imodzi yokha.
- Phatikizani marikisi onse a pa mwezi ndipo lembani kumapeto pa malo amene mwapatsidwa.

N'kofunika kusaumira ndi kuchita chilichonse chothandiza kulimbikitsa ophunzira kuti aphunzire Baibulo lawo. N'zothandizanso kuti kumapeto kwa mwezi uliwonse mphunzitsi azilemba mawu a chilimbikitsa kwa wophunzira pa malo amene aperekedwa. Mutha kulemba ndemanga yoyamikira kuchekenira bwino, zilembo zabwino ndi kumvetsa bwino phunziro ndi zina zambiri.

Yesetsani kuti ndemanga, mafunso, ziganizo, zomwe mwaona ndi zina zambiri zikhale zosiyanasiyana, kuti zithandize kupanga zinthu kukhala zosiyana. Izi zimafunika kuganiza bwino, ndipo ndi kofunika kuti wophunzira azikhala ndi chidwi nthawi zonse. Ngati chiganizo chomwecho kapena funso lomwe likubwera mwezi uliwonse, zimachotsa chidwi cha wophunzira.

Kalasi Yoyamba

Ndemanga zina

“Chikondi – Ine ndasangalala kuti inu mwayamba maphunziro awa ndipo ndikukhulupirira kuti muwakonda. Zochekenira zanu ndazikonda. Kodi mumapita ku sukulu? Ndikuyembekezera kumva kuchokera kwa inu posachedwa”

“Wachita bwino, Andrey. Wachekenira bwino kwambiri! Kodi zimavuta pamene mumachekenira mizere ya m'kati? Inu musiyako zochepa zokha munachekenira pang'ono phunziro lapita lija.”

Ndemanga zauzimu

“Wachita bwino, Sarah. Yairo analitu munthu wokondwa kwambiri pamene Yesu anamuthandiza.”

“Yankho labwino kwambiri! Nkhani ya kufa kwa Yesu ndi yomvetsa chisoni, koma chokondweretsa ndi chakuti lye anaukanso.”

Kalasi Yachiwiri

Ndemanga zina

“Yankho labwino, Chimwemwe – Ine ndikukhulupirira kuti aphunzitsi ako akusangalala kwambiri ndi ntchito yako ku sukulu!”

“Ine ndikudziwa kuti posachedwapa ndi tsiku lako lobadwa, Chisomo. Kodi udzachita phwando? Udzachitira kuti? Udzakhale ndi tsiku lopambana kwambiri!”

“Iwe wayesetsa kwambiri. Pali zolakwika zochepa chabe. Usamayiwale kuonanso mayankho nthawi iliyonse.”

Ndemanga zauzimu

“Ine ndasangalala ndi mmene wachekenira chithunzi cha Yesu ali nkhandu modyera ng'ombe. Kodi sizinali zabwino kuti Mulungu atumize Mwana wake ku dziko lapansi kwa ife?”

“Mitundu yako ndayikonda kwambiri! Zekariya anapereka dipo chifukwa cha kusankhulupirira zimene Mulungu ananena. Iye anakayikiranso Mawu a Mulungu.”

“Mayankho abwino kwambiri. Munthu amene anakumana ndi Filipo ku chipululu anapita kwawo akusangalala kwambiri. Iye anamva ndi kukhulupirira nkhani yabwino ya Yesu.”

Zoonjezera A - Kalasi 0 ndi 1 Zinthunzi Zaulelele m'Baibulo

	Mutu	Nkhani m'Chithunzi
A1	Chilengedwe	Mulungu alenga dziko lapansi
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/rp-faith-hebrews-11-a/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-creation/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/lc-creation-days/
		Mulungu analenga nyama ndi anthu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/fl-adam-eve/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/lc-creation-days/
		Mwamuna ndi mkazi woyamba
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/fl-adam-eve/
		Dziko la Mulungu lawonongedwa
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/fl-adam-eve/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/isc-objects/
A2	Nowa	Nowa amvera Mulungu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/lc-noah-ark/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/btbn-noah/
		Kupulumuka m'Chombo
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/lc-noah-ark/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/btbn-noah/
		Kuyamba mwatsopano
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/lc-noah-ark/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/isc-animals/
		Lonjezo la Mulungu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/lc-noah-ark/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/isc-objects/
A3	Petulo	Yesu ayitana Petulo
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/lc-peter-fishing/
		Yesu athandiza Petulo
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/lc-peter-fishing/
		Yesu aletsa mphepo yamphamvu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/lc-jesus-storm/
		Yesu apulumutsa Petulo
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/lc-peter-water/

Zoonjezera B - Kalasi 0 ndi 1 Zinthunzi Zauzelele m'Baibulo

	Mutu	Nkhani m'Chithunzi
A4	Petulo - Mtanda	Petulo agona tulo
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-jesus-arrested/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-easter/
		Petulo adula khutu la munthu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-jesus-arrested/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-judas/
		Petulo anama za Yesu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-jesus-arrested/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-jesus-trial/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-jesus-high-priest/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-peter-rooster/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-easter/
		Petulo ayankhula ndi Yesu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-easter/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-resurrection-breakfast/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-thomas-doubts/
A5	Abrahamu	Abrahamu achoka kwawo
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-ur-preschool/
		Abrahamu ndi Loti
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-lot-preschool/
		Malonjezo a Mulungu kwa Abrahamu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-abraham-sarah/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-abram/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/abram-hagar-preschool/
		Abrahamu ndi alendo
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-abraham-sarah/
A6	Abrahamu	Abrahamu amvera Mulungu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-abraham-isaac/
		Chisamaliro cha Mulungu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/abram-hagar-preschool/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-lot-preschool/
		Thandizo la Mulungu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-isaac-wife/
		Chisankho cha Mulungu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-isaac-wife/

Zoonjezera A - Kalasi Yachiwiri Zinthunzi Zaulelele m'Baibulo

	Mutu	Nkhani m'Chithunzi
A1	Chilengedwe	Mulungu alenga dziko lonse
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/creation/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-creation/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-creation-days/
		Mulungu alenga dziko lapansi ndi munthu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/creation/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/fl-adam-eve/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-creation-days/
		Mwamuna woyamba ndi mkazi woyamba
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/creation/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/fl-adam-eve/
		Kuonongeka kwa dziko la Mulungu
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/adam-eve-fall/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/fl-adam-eve/
A2	Nowa	Nowa amvera Mulungu
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/
		Kutetezedwa m'Chombo
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/
		Kuyamba mwatsopano
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/
		Lonjezo la Mulungu
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/noah-ark/
A3	Petulo	Yesu ayitana Petulo
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/andrew-philip-nathanael/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-015-first-disciples/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-022-four-disciples/
		Yesu athandiza Petulo
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-jesus-fishermen/
		Yesu aletsa namondwe
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-storm/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-043-jesus-storm/
		Yesu apulumutsa Petulo
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-water/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-054-walking-water/

Zoonjezera B - Kalasi Yachiwiri Zinthunzi Zaulelele m'Baibulo

	Mutu	Nkhani m'Chithunzi
A4	Petulo - Mtanda	Petulo akugona
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-089-prayer-garden/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/gethsemane-peter/
		Petulo achita ndewu
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-085-judas-betrays/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/gethsemane-peter/
		Petulo akana Yesu
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-087-last-supper/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-090-trial-begins/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-091-peter-denials/
		Petulo akonda Yesu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-105-peter-restored/
		https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-questions-peter/
A5	Abrahamu	Mulungu ayitana Abram
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-canaan/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/rp-abraham-calling/
		Abramu ndi Loti
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-lot/
		Malonjezo a Mulungu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-promise/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-strangers/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/rp-faith-hebrews-11-b/
		Abrahamu ndi alendo
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-strangers/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-isaac/
A6	Abrahamu	Abrahamu amvera Mulungu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-abraham-isaac/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-isaac/
		Abrahamu amvera Mulungu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-abraham-isaac/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/abraham-isaac/
		Thandizo la Mulungu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/isaac-wife/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-isaac-wife/
		Chisankho cha Mulungu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/isaac-wife/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-isaac-wife/



© Bible Educational Services 2020

www.besweb.com

Registered Charity UK CIO 1186004

NY - 02/2023
(Chichewa)